# Kumvetsetsa Kuti Kodi Yesu Ndi Ndani? Kusiyana kwa maganizo a Asilamu ndi Akhristu



GUÐRÚN MARGRÉT PÁLSDÓTTIR

# Kumvetsetsa Kuti Kodi Yesu Ndi Ndani?

## Kusiyana Kwa Maganizo a Asilamu ndi Akhristu

# Kumvetsetsa Kuti Kodi Yesu Ndi Ndani?

## Kusiyana kwa maganizo a Asilamu ndi Akhristu

**Guðrún Margrét Pálsdóttir**

Dzina La Bukhuli Mu Chingerezi: The Understanding of Who Jesus Is: The Basic Difference Between Muslims and Christians
Chichewa translation – Wotanthauzira Chichewa

© Copyright 2021 - Guðrún Margrét Pálsdóttir
Wotanthauzira:  Fatsani MK Mwale
Wokonza Chikutiro: Karousel ehf – María Ericsdóttir Panduro
Wofalitsa: WJI Publishing
Wosindikiza Chichewa: 2022

Bukhu ili likhodza kusindikizidwa ndi kumasulilidwa mu zilankhulo zina koma lisapangidwire phindu.  Dziwitsani mlembi za izi polembera e-mail ku: understanding@whojesus.is

Khalani omasuka kuwerenga kapena kugawira ena bukhuli.  Mukhodza kulipeza la m'chingerezi pa makina a kompyuta mukapita pa website iyi: **whoJesus.is**

Mau a mu Koran atengedwa kuchokera mu:

Qur'an Yolemekezeka Yotanthauzidwa M'chichewa yosindikizidwa ndi Nyumba ya Mfumu Fahd.
Womasulilidwa ndi Sheikh Khalid Ibrahim
Pansi pa alembi: Sheikh Abdallah Omar Issa Mdala ndi Sheikh Shaibu Muhammad Mzoma (1999).

Mau a Baibulo achokera mu Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu (2014).

Lopita ku dziko lonse lapansi

Loyamba linasindikizidwa ku Iceland

ISBN 978-9935-526-22-9 (Logulitsidwa msitolo)
ISBN 978-9935-526-23-6 (la PDF)

# Loperekedwa Kwa

*Cholinga Changa*
*Ndikufuna kupereka bukhuli kwa anzanga onse*
*Achisilamu ku Iceland*
*ndi*
*ena onse padziko lapansi*
*amene afunafuna choonadi*

# Za M'katimu


Mau Oyamba …………………………………………………..………..…9

Malonje ………………………………………………………..……...…11

Mutu 1: Mbali Zosiyana Za Yesu Mu Mabuku Awiriwa ……..……….13

Mutu 2: Kodi Yesu Anafadi Pamtanda? ………………………………21

Mutu 3: Kodi Yesu ndi Mwana Wa Mulungu? ……………..………..33

Mutu 4: Kodi Yesu ndi Mulungu? ……………………………………41

Mutu 5: Kodi Yesu ndi Mpulumutsi Wa Dziko Lapansi? ……….……49

Mutu 6: Kodi Yesu ndi Mkhalapakati Pa Mulungu ndi Munthu? ...…..55

Mutu 7: Kudalilika Kwa Mabuku Awiriwa …………………..……59

Mau Omaliza……………………………………………..……………64

Maina A Yesu Mu Koran ndi Mu Baibulo……………………..……65

Ziphunzitso Zina Za Yesu ……………………………………..………66

Mabuku Amene Anagwiritsidwa Ntchito Pa Kafukufuku …………....67

# Mau Oyamba

Sikolakwikwa kuganiza kuti anthu ambiri owerenga bukhuli amanena kale kuti ife Yesu timamudziwa kuchokera mu zimene iwo anawerenga za iye kuchokera mu Baibulo kapena Koran kapenanso pa zimene iwo anangomva za iye.

Bukhuli likupereka mwayi wakuti anthu adziwe mbali zonse. Munthu akangodziwa mbali imodzi pamakhala povuta kuti amvetsetse. Zimatengera kulimba mtima kuti munthu awunike pa zinthu zimene iye sakuzidziwa kapena kuzimvetsa bwino ndipo pakutero munthu umatha kutsimikizira kuti zimene umakhulupilira ndi choonadi kapenanso umatha kutsutsidwa kuti maziko a chikhulupiliro chako ali pa mchenga osati choonadi.

Ndimakonda kwathunthu Asilamu, Akhristu, Ayuda ndi anthu a zipembedzo zina koma pamwamba pa zonsezi ndimakonda choonadi. Iyi ndiye ngodya imene ndikufuna kumangapo moyo wanga. Mwa ichi ndawerenga Koran ndi Baibulo. Cholinga change polemba bukhuli ndikufuna kugawana nanu mfundo zikuluzikulu zimene mabuku awiriwa, Baibulo ndi Koran, analemba za Yesu.

Ndi pemphero langa kuti muwerenge bukhuli ndi malingaliro otseguka ndi ofuna kufunafuna kudziwa choonadi.

*Guðrún Margrét Pálsdóttir (Gunna Magga)*

# Malonje

Ayuda, Akhristu ndi Asilamu onse amakhulupilira Mulungu kuti ndi m'modzi ndipo onse amakhulupilira za atumiki monga Abrahamu, Mose ndi aneneri ena akale.

Akhristu amakhulupilira Baibulo la Ayuda ndipo amalitchula kuti Chipangano Chakale poti iwo anawonjezera mu Baibulo la Chiyudali Chipangano Chatsopano chimene chimakamba za kudza kwa Mesiya, Moyo wake ndi chiyambi cha mpingo.

Asilamu amakhulupilira Koran imene imakamba za nkhani zina za mu Chipangano Chakale ngakhale pena ndi pena mosiyaniranako.

Koran imanena za bukhu/malemba (Baibulo) ndi za anthu a m'bukhu (Ayuda ndi Akhristu) za Yesu ngati Mesiya (Khristu).

Baibulo liri ndi maulosi oposa 300 okamba za Mesiya amene ambiri anakwaniritsidwa mu Chipangano Chatsopano ndi Yesu pa moyo wake monga mwa zimene omwe adali naye anaona akuzichita.

Kuonjezera apa, olemba mbiri yakale yadziko a mu zaka za 100 ndi 200 analemba za mbiri ya Yesu mofana ndi zimene timazipeza mu Baibulo.

Asilamu ndi Akhristu amavomereza kuti Yesu ndiye Mesiya pamene Ayuda ambiri sadavomerezebe ndipo mpaka pano iwo ati akudikilirabe Mesiya.

Ngakhale kuti Yesu anali mu Yuda ndi kuti ophunzira ake oyamba onse anali Ayuda, iye anakanidwa, nazengedwa mlandu ndi kupachikidwa ndi anthu achipembedzo ati chifukwa chonyoza Mulungu. Ayuda ena ochuluka masiku ano akuzindikira kuti Yesu ndiyedi Mesiya.

Mu bukhuli ndifuna kuonetsa kuti kodi Yesu amene amapatsidwa ulemu waukulu ndi Asilamu ndi kupembedzedwa ndi Akhristu ndi ndani?

# *Mutu 1:*

# Mbali Zosiyana Za Yesu Mu Mabuku Awiriwa

**Baibulo ndi Koran zimagwirizana pa zinthu izi:**

Kuti Yesu ndi Mesiya, Mneneri, Mau a Choonadi, Mau a Mulungu. Amatha kuchiritsa odwala, kuonetsa akhungu ndi kuukitsa akufa. Kubwera kwake kudziko kunalengezedwa ndi Angelo, nabadwa mwa namwali ndipo kuti kubadwa kwake kunali kodabwitsa ndi kuti anakwera kunka kumwamba ndipo kuti ali ndi moyo ndipo adzabweranso.

**Koran** imati Yesu ndi Mesiya koma siinena tsatanetsatane za udindo wa Mesiya kuti ukutanthauzanji monga mwa zomwe aneneri a m'Chipangano Chakale adalembera. Koma pa *Koran 10:94* ndi *16:43* analemba kuti ngati anthu sakudziwa kapena kuti pali chikayiko china chake ndi bwino kuti apeze mayankho mu Baibulo kapena kwa iwo amene adaliwerenga.

Tatiyeni tione mwa tsatanetsatane zomwe aneneri akalewa analosera za Mesiya kunena za kubadwa kwake, ntchito yake ndi imfa yake. Zonsezi zinakwaniritsidwa ndi Yesu monga taonetsera pansipa.

Izi zonse zikupezeka mu mabukhu a Uthenga Wabwino komanso ngakhale zina zilipo mu Koran.

**Maulosi ndi Kukwaniritsidwa Kwake:**

| Chochitika | Ulosi/Uneneri | Kukwaniritsidwa Kwake |
|---|---|---|
| Kuti adzabadwa mwa Namwali | *Yesaya 7:14* ndi *Yesaya 9:1-7* | *Mateyu 1:18-25, Luka 1:26-38, Koran 19:19-22* |
| Kuti adzabadwira ku Betelehemu | *Mika 5:2* | *Mateyu 2:1-11, Luka 2:1-7* |
| Kuti adzabweretsa kukhululukira, machiritso ndi kupenyetsa akhungu | *Yesaya 42.6-7; 61.1-3; Zekariah 13.1* | *Marko 2.1-12,17; Luka 4.14-21; 6.19; 7.21-22; 11.5-6; 18.35-43; Koran 3.49* |
| Adzadzichepetsa – Mfumu yokwera pa bulu | *Zekariah 9.9* | *Mateyu 27.37; Marko 11.7-10* |
| Adzagulitsidwa pa mtengo wa ndalama makumi atatu | *Masalmo 41.10; Zekariah 11.12-13* | *Mateyu 26.14-15; 27.3-10* |
| Kuti adzamenyedwa, kunyozedwa ndi kulavulilidwa | *Yesaya 50.6* | *Mateyu 26.67; 27.26; Marko 14.65* |
| Kuti Adzapachikidwa | *Masalmo 22.1-19* | *Mateyu 27.22-44; Marko 15.16-41; Luka 23.22-49; Yohane 19.1-37* |
| Kuti adzafera machimo athu | *Yesaya 53.4-12* | *Mateyu 26.28; 1 Petro 2.24* |
| Kuti padziko lonse padzagwa mdima nthawi yakufa kwake | *Amosi 8.9-10* | *Mateyu 27.45, Marko 15.33, Luka 23.44* |
| Kuti adzakhala kuunika kwa dziko lapansi | *Yesaya 9.2,6; 60.1-3* | *Yohane 1.4,9; 12.46* |

**Zimene Yesu adanena za iye yekha monga analembera wophunzira wake Yohane:**

*"Ine ndine mkate wamoyo, Iye amene adza kwa ine sadzamva njala ndi iye amene akhulupilira ine sadzamva ludzu nthawi zonse." (Yohane 6:35)*

*"Ine ndine kuunika kwa dziko lapansi, iye wonditsata ine sadzayenda mu mdima koma adzakahala nako kuunika kwa moyo." (Yohane 8:12)*

*"Ine ndine khomo ngati wina alowa ndi ine adzapulumutsidwa, nadzalowa, nadzatuluka nadzapeza busa." (Yohane 10:9)*

*"Ine ndine kuuka ndi moyo, wokhulupilira ine angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo." (Yohane 11:25)*

*"Ine ndine Njira, choonadi ndi moyo, palibe munthu adza kwa Atate koma mwa ine." (Yohane 14:6)*

*"Ine ndine mbusa wabwino, mbusa wabwino ataya moyo wake chifukwa cha nkhosa." (Yohane 10:11)*

*"Ine ndine muzu ndi mbadwa ya Davide, nyenyezi yonyezimira ya nthanda." (Chibvumbulutso 22:16)*

*"Ine ndine Alefa ndi Omega, Woyamba ndi Wotsiriza, Chiyambi ndi Chitsiriziro." (Chibvumbulutso 22:13)*

*"Inu ndinu ochokera pansi ine ndine wochokera kumwamba, inu ndinu a dziko lino lapansi sindili ine wadziko lino lapansi." (Yohane 8:23)*

*"Ngati mukhala inu mmau anga muli akuphunzira anga ndithu ndipo mudzazindikira choonadi ndipo choonadi chidzakumasulani." (Yohane 8:31-32)*

*"Lamulo langa ndi ili kuti mukondane wina ndi nzake monga ndakonda inu. Palibe munthu ali nacho chikondi choposa ichi, chakuti munthu ataya moyo wake chifukwa cha abwenzi ake." (Yohane 15:12-14)*

**M’ndandanda Woonetsa Kusiyana Kwa Zikhulupiliro Zakuti Yesu ndi Ndani?**

| YESU | Mesiya mu Chipangano Chakale | Yesu mu Chipangano Chatsopano | Yesu mu Koran | Kutsimikizira a kwa akatswiri a mbiri yakale |
|---|---|---|---|---|
| **Wobadwa mwa namwali** | Inde<br>*Yesaya 7.14* | Inde<br>*Mateyu 1.18-23*<br>*Luka 1.26-38* | Inde<br>*Koran 19.19-22* | |
| **Ndi m’neneri** | Inde<br>*Deuteronomo 18.18; 34.10-12* | Inde<br>*Machitidwe 3.20-22*<br>*Mateyu 13.57; 21.11* | Inde<br>*Koran 19.30* | Inde<br>*Lucian* 1) |
| **Ndi Mau a Mulungu** | | Inde<br>*Yohane 1.1-14* | Inde<br>*Koran 3.45* | |
| **Ndi Mau a Choonadi/ Ndiye Choonadi** | | Inde<br>*Yohane 14.6* | Inde<br>*Koran 19.34* | |
| **Ndiye kuunika kwa dziko lapansi** | Inde<br>*Yesaya 9.2; 60.1-3* | Inde<br>*Yohane 1.4,9; 12.46* | | |
| **Anachiza odwala** | Inde<br>*Yesaya 61.1; 53.5* | Inde<br>*Luka 8.43-48*<br>*Mateyu 9.35; 21.14* | Inde<br>*Koran 3.49* | |
| **Anapenyetsa akhungu** | Inde<br>*Yesaya 42.6-7* | Inde<br>*Luka 7.21-22* | Inde<br>*Koran 3.49* | |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **Anaukitsa akufa** | | Inde<br>*Luka 8.49-55* | Inde<br>*Koran 3.49* | |
| **Anachita zozizwitsa zambiri** | Inde<br>*Yesaya 35.4-6* | Inde<br>*Marko 7.32-37* | Inde<br>*Koran 3.49* | Inde<br>*The Babylonian Talmud* 2),<br>*Josephus* 3) |
| **Ndi Mwana wa Mulungu** | Inde<br>*Masalmo 2.7,12* | Inde<br>*Yohane 3.16*<br>*1 Yohane 1.3* | Ayi<br>*Koran 19.88-92* | Analambirid wa ngati Mulungu atauka kwa akufa:<br>*Pliny the Younger* 4),<br>*Lucian* |
| **Ndi Mesiya / Khristu** | Inde<br>*Yesaya 9.1-7; 61.1-3* | Inde<br>*Mateyu 2.1-5* | Inde<br>*Koran 3.45* | Inde<br>*Tacitus* 5),<br>*Pliny the Younger,*<br>*Josephus* |
| **Ndi Mpulumutsi** | Inde<br>*Yesaya 35.4-6* | Inde<br>*Luka 2.10-11*<br>*Mateyu 20.28* | Ayi<br>*Koran 3.84* | |
| **Anakhululukira machimo** | Inde<br>*Yesaya 1.18; 53.3-12* | Inde<br>*Marko 2.5-12*<br>*Mateyu 1.21* | Ayi<br>*Koran 5.75* | |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **Ndi m'khala pakati pa Mulungu ndi munthu** | Inde<br>*Yesaya 42.6* | Inde<br>*1 Timoteo 2.5* | Ayi<br>*Koran 2.255* | |
| **Iye mwini ndiye Mulungu** | Inde<br>*Yesaya 9.6-7; 35.4-5* | Inde<br>*Yohane 1.1; 20.28-29* | Ayi<br>*Koran 5.72* | |
| **Anabatizidwa** | | Inde<br>*Mateyu 3.13-17* | | Inde<br>Ambiri amavomereza |
| **Anapachikidwa** | Inde<br>*Masalmo 22.2-19* | Inde<br>*Mateyu 27.32-50*<br>*Marko 15.1-37*<br>*Luka 23.13-46*<br>*Yohane 19.1-30* | Ayi<br>*Koran 4.157* | Inde<br>Ambiri amavomereza<br>Mabuku akale:<br>*Lucian, Tacitus, Josephus, Babylonian Talmud* |
| **Anaikidwa m'manda** | Inde<br>*Yesaya 53.9* | Inde<br>*Mateyu 27.57-66* | | Inde<br>Ambiri amavomereza |
| **Anauka kwa Akufa** | Inde<br>*Yesaya 53.10*<br>*Masalmo 16.10; 49.16* | Inde<br>*Mateyu 28.1-15*<br>*Marko 16.1-7*<br>*Luka 24.1-7*<br>*Yohane 20.1-18*<br>*Machitidwe 2.22-27* | Inde<br>*Koran 19.33* | Inde<br>Ambiri amavomeleza.<br>Mabuku akale:<br>*Josephus, Tacitus* |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **Anakwera kunka Kumwamba** | Inde *Masalmo 68.18; Danieli 7.13-14* | Inde *Machitidwe 1.9* | Inde *Koran 3.55; 4.158* | |
| **Lero lino ndi wamoyo** | Inde *Yesaya 9.6-7* | Inde *Mateyu 28.18-20; Chibvumbulutso 1.12-18* | Inde *Koran 4.158* | |
| **Adzabweranso** | Inde *Danieli 7.13-14* | Inde *Yohane 14.2-3; Machitidwe 1.9-11; Chibvumbulutso 1.7* | Inde *Koran 4.159; 43.61* | |

**Kusiyana kwakukulu pakumvetsetsa zakuti Yesu anali ndani pakati pa Asilamu ndi Akhristu kukhoza kuunikidwa mu mafunso otsatirawa:**

- Kodi Yesu anafadi pa mtanda?
- Kodi Yesu ndi Mwana wa Mulungu?
- Kodi Yesu ndi Mulungu?
- Kodi Yesu ndi Mpulumutsi wa dziko lapansi?
- Kodi Yesu ndiye m’khala pakati pa Mulungu ndi munthu?

Mu Koran, mayankho a mafunso onsewa ndi **ayi** pamene mu Baibulo mayankho onse pa mafunsowa ndi **inde.** Tiyeni tione mwatsatanetsatane poyankha funso liri lonse palokha.

*Mutu 2:*

# Kodi Yesu Anafadi Pamtanda?

**Koran imaphunzitsa kuti Yesu sanapachikidwe pa mtanda:**

*Ndikulankhula kwao (kwakuti), "ife, tamupha Mesiya, Yesu, mwana wa Maria, mtumiki wa Mulungu. Koma sadamuphe, ndipo sadampachike pa mtanda. Koma adasokonezedwa (ndi munthu wina namuganizira kuti ndi Yesu). Ndithudi amene akutsutsana pa nkhani (yakuphedwa kwake) ali m'chikaiko ndi kuphedwa kwake; alibe kudziwa kotsimikizika, koma akungotsatira zongoganizira ndithudi sadamuphe. Koma Mulungu adamukweza kwa iye yekha... (Koran 4.157-158)*

Ngakhale izi zili chonchi, ndime zina za Koran zimavomeleza kuti Yesu adafa ndi kuuka kwa akufa.

Korani imati Yesu anayamba kulankhula patangotha masiku awiri atangobadwa kunena kuti iye adzamwalira:

*[Mwanayo adanena], "Ine ndine kapolo wa Mulungu. Wandipatsa bukhu ndikundichita kukhala mneneri. Ndipo wandichitaa kukhala wodala paliponse pomwe ndili ndipo wandilamula kuswali ndi kupereka zakat pomwe ndili moyo." (Koran 19.30-31)*

*"Ndipo mtendere uli pa ine kuyambira patsiku lomwe ndidabadwa kufikila tsiku limene ndidzamwalira ndi tsiku limene ndidzaukitsidwa (kwa akufa pa tsiku la chiweruzo) ndikukhala ndi moyo." (Koran 19.33)*

Mavesi ena awiri amati Yesu anali atafa kale, ngakhale kuti mabuku ena a chizungu a Koran sanena mwatchutchutchu za izi:

*[Kumbukirani] pamene Mulungu adati, "Iwe Yesu, ine ndikukwanilitsira nyengo yako yokhala ndi moyo (Ayuda sachita kanthu pa iwe). Ndikunyamulira kwa ine ndikuyeretsa kwa anthu osakhulupilira (omwe ndi adani ako). Ndipo owe akutsata iwe ndiwasankha kukhala a pamwamba kufikila tsiku la chimaliziro. Kenako kobwerera kwanu nkwa ine ndipo ndidzaweruza pakati panu pa zomwe mudali kusiyana." (Koran 3.55)*

Ma Korani ena amasulira ndimeyi momveka bwino kuti:

*Ndipo pamene Allah anati: "Iwe Yesu, Ndidzathetsa nthawi yakukhala kwako [pa dziko]..."* (M.H. Shakir translation)

Mau a chiluya (chi Arabu) amene agwritsidwa ntchito mu vesili (kutanthauzidwa kuti kuthetsa) ndi *mutawaffeeka* amene akhoza kuthandauza kufa, monga amakonda kugwiritsidwira ntchito, kapena kuti anapita kwa Mulungu mu tulo kenako mkubwerereranso m'thupi lake.
Mau ngati omwewa agwiritsidwanso pa Koran 5.117 – pamene akuti, "Munandikweza m'mwamba":

*Sindidanawauze chilichonse kupatula chomwe munandilamulira kuti – pembedzani Mulungu, Mbuye wanga komanso Mbuye wanu. Ndipo ndinali mboni kwa iwo pamene ndinali nawo; Koma pamene mudanditenga, Inu ndiye munali muyang'aniri pa iwo; ndipo Inu ndinu mboni yachilichonse. (Koran 5.117)*

Mau a chingerezi pa ma vesi awiriwa anasintha tanthauzo leni la mau a chi Arabu akuti *kufa*.

| **Mtundu wa Koran** | **Koran** | **Vesi** |
|---|---|---|
| M. Muhammad Ali 1917 | 3:55 | *"... Ndidzakupangitsa kuti ufe ndikukukweza pamaso panga..."* |
| | 5:117 | *"... Koma pamene munadipangitsa kuti ndife..."* |
| Sher Ali 1955 | 3:55 | *"... Ndidzakupangitsa kuti ufe imfa ya chilengedwe ndikukukweza kwa ine Mwini..."* |
| | 5:117 | *"Koma kuyambira pamene munandipangitsa kuti ndife..."* |
| M.H. Shakir 1983 | 3:55 | *"... Ndidzathetsa nthawi yakukhala kwako pa dziko lapansi ndikukukweza kuti ukwere kwa Ine…"* |
| | 5:117 | *"...Koma pamene munandipangitsa kuti ndife…"* |
| Muhammad Asad 1980 | 3:55 | *"... Ndikuuzitsani, Ndidzapangitsa kuti ufe ndipo ndidzakukweza kwa ine..."* |
| | 5:117 | *"... Koma poti munapangitsa kuti ndife..."* |
| Rashad Khalifa 1981 | 3:55 | *"... Ndikupha (ndikuthetsa moyo wako), kukukweza kwa ine..."* |
| | 5:117 | *"... Pamene munathetsa moyo wanga padziko ..."* |
| Mohammad & Osama El-Shinawy 1978 | 3:55 | *"... O Issa, Zoonadi ndidzakutenga ndi kukukweza kwa ine ndekha..."* |
| | 5:117 | *"... Koma pamene munandikweza m'mwamba..."* |

Kuonjezera apo, Koran imanenanso kuti Yesu anafa monga m'mene atumiki ena onse a Mulungu anafera:

*Muhammad Sali chinthu china koma mtumiki chabe. Patsogolo pake adamuka atumiki ambiri… (Koran 3.144)*

**Chipangano Chatsopano cha Baibulo chili ndi mbiri ya kupachikidwa ndi imfa ya Yesu pa mtanda imene olemba ake ambiri ndi oti anaona zikuchitika.**

Izi tikhoza kuziwerenga pa: *Mateyu 27.1-56; Marko 15.1-41; Luka 22.47-23.49* and *Yohane 18.1-19.37.* Amafotokoza za momwe Yesu anamugwirira, kumuzenga milandu, kumenyedwa, kuvekedwa chisoti cha minga, kunyozedwa, kulavulilidwa ndi asilikali a chi Roma ndi mmene anamuweruzira kuti akapachikidwe pa mtanda. Amafotokozeranso za ulendo wonse wonka ku Gologota, mmene misomali inakhomedwera pathupi lake (mmanja ndi mapazi) ndi mmene anamubayira m'nthiti pofuna kutsimikizira za kuti anamwaliradi. Kuonjezera apa maina a anthu ena omwe analipo pakupachikidwako analembedwa bwino lomwe.

**Mabuku a Uthenga Wabwino amanenanso za zimene Yesu analankhula ali chikhomedwere pa mtanda:**

- Anapempha Mulungu kuti awakhululukire iwo amene ankamupachika popeza samadziwa chimene amachita. (*Onani Luka 23.34)*
- Analonjeza mmodzi wa achifwamba wopachikinidwa naye pamodzi kuti lero lomwe lino adzakhala naye m'paradizo. *(Onani Luka 23.43)*
- Anafunsa Mulungu kuti chifukwa chiani adamusiya yekha. *(Onani Mateyu 27.46; Marko 15.34)*
- Anauza a Mayi ake Mariya kuti tsopano wophunzira wake Yohane ndi mwana wake ndipo anauzanso Yohaneyo kuti atenge Mariya kukhala mayi ake. *(Onani Yohane 19.26-27)*
- Ananena kuti akumva ludzu. *(Onani Yohane 19.28)*
- Anasonyeza kuti ntchito yake pa dziko lapansi yatha ndi kukwaniritsidwa ponena kuti:
  *"Kwatha!" (Yohane 19.30)*
- Ndipo pomwalira iye anati, *"Atate, mmanja mwanu ndipereka mzimu wanga." (Luka 23.46)*

**Nkhani za mu mabuku a Uthenga Wabwino zimafotokozeranso bwino za zina zimene zidachitika pa tsiku limene Yesu adapachikidwa pa Mtanda:**

*"Ndipo ola la chisanu ndi chimodzi panali mdima pa dziko lonse kufikira ola la chisanu ndi chinayi…Ndipo Yesu pamene anafuula ndi mau aakulu anapereka mzimu wake ndipo onani, chinsaru chotchinga cha mu kachisi chinag'ambika pakati kuchokera ku mwamba kufikira pansi; ndipo dziko linagwedezeka ndi miyala inang'ambika, ndi manda anatseguka, ndi mitembo yambiri ya anthu oyera mtima akugona kale, inauka…Ndipo anali naye akudikila Yesu, anaona chivomerezi ndi zinthu zimene zinachitidwa, anaopa kwambiri, nanena, Indedi uyu ndiye Mwana wa Mulungu!" (Mateyu 27.45, 50-52, 54)*

**Dziwani! Mabukhu a Uthenga Wabwino analembedwa ndi anthu amene anaziona zinthuzi mu nthawi imene anthu ambiri amene adazionanso adakali ndi moyo ndipo amakumbukira tsatane lomwe za zomwe zidachitika.**

**Aneneri a Chipangano Chakale analosela za imfa ya Mesiya ndipo anafotokozera chifukwa chimene adzafere ndi mmene adzaphedwere:**

Masalmo 22 amayamba ndi mau omwe Yesu anafuula pa mtanda:
*Mulungu wanga, Mulungu wanga mwandisiyiranji ine? (Masalmo 22.1)*

Salmo limeneli limafotokoza tsatanetsatane za zimene zidachitika pamene Yesu anapachikidwa pa mtanda koma linalembedwa zaka 1000 zinthuzo zisadachitike:

*Ndathiridwa pansi monga madzi ndipo mafupa anga onse anaguluka. Mtima wanga ukunga sera; wasungunuka mkati mwa matumbo anga. Mphamvu yanga yauma ngati phale ndi lilime langa likangamira kunsaya zanga; ndipo mwandifikitsa ku fumbi la imfa. Pakuti andizinga agalu, msonkhano wa oipa wanditsekereza, andiboola m'manja anga ndi mapazi anga. Ndikhoza kuwerenga mafupa anga onse, iwo ayang'ana*

*nandipenyetsetsa ine. Agawana zovala zanga, nachita maere pa Malaya anga. (Masalmo 22.14-18)*

Uthenga Wabwino wolembedwa ndi Yohane umafotokozera m'mene ulosiwu unakwaniritsidwira ngakhale zimene anachita ndi Malaya a Yesu: *Pamenepo asilikali mmene adapachika Yesu, anatenga zovala zake, anadula panai, natenga wina china wina china ndiponso Malaya; koma Malaya anaombedwa monsemo kuyambira pamwamba pake analibe msoko. Chifukwa chake anati wina ndi nzake, "Tisang'ambe awa koma tichite maere, awa akhale a yani" kuti lembo likwaniridwe limene linena, "anagawana zovala zanga mwa iwo okha, ndi pa Malaya anga anachitira maere." Ndipo asilikali anachita izi. (Yohane 19.23-24)*

Mneneri Yesaya akufotokozera pa mutu 53 chifukwa chimene Mesiya ati adzafere:
*Iye ananyozedwa ndi kukanidwa ndi anthu, munthu wazisoni ndi wodziwa zowawa; ndipo ananyozedwa monga munthu wombisira anthu nkhope zao; ndipo ife sitinamlemekeze. Zoonadi iye ananyamula zowawa zathu ndikusenza zisoni zathu; natunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu koma ife tinamuyesa wokhomedwa, wokanthidwa ndi Mulungu, ndi wobvutidwa. Koma iye analasidwa chifukwa cha zolakwa zathu, natunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu; chilango chotitengera ife mtendere chinamgwera iye ndipo ndi mikwingwirima yake ife tachiritsidwa. Tonse tasochera ngati nkhosa, tonse tayenda njira ya mwina yekha; ndipo Yehovah anayika pa iye mphulupulu ya ife tonse…Anachotsedwa ku chipsinjo ndi chiweruziro, ndipo ndani adafotokoza nthawi ya moyo wake? Pakuti walikhidwa kunja kuno, chifukwa cha kulakwa kwa anthu anga iye anakhomedwa. (Yesaya 53.3-6, 8)*

**Yesu anawuza akuphunzira ake za imfa yake ndi kuuka kwake:**
*Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kuwalangiza akuphunzira ake, kuti kuyenera iye amuke ku Yerusalemu kukazunzidwa zambiri ndi akulu ndi akulu a nsembe ndi alembi, ndi kukaphedwa, ndi tsiku lachitatu kuuka kwa akufa. (Mateyu 16.21)*

*Ndipo pamene Yesu anali kukwera kunka ku Yerusalemu, anatenga ophunzira khumi ndi awiri napita nawo paokha, ndipo pa njira anati kwa iwo, Onani tikwera ku Yerusalemu, ndipo mwana wa munthu adzaperekedwa kwa ansembe akulu ndi alembic ndipo iwo adzamuweruza kuti ayenera imfa, nadzampereka kwa anthu a kunja amunyoze ndi kumkwapula, ndi kumpachika ndipo iye adzaukitsidwa pa tsiku lachitatu." (Mateyu 20.17-19)*

Onaninso pa: *Mateyu 12.38-40; 16.1-4; 17.22-23; Marko 8.31-32; 9.31; 10.33; Luka 9.22.*

**Imfa ya Yesu ndi imodzi mwa mbiri zolembedwa bwino mu mbiri yakale ya dziko la pansi,** osati chifukwa choti mabuku anayi a Uthenga wabwino anafotokozera tsatanetsatane koma chifukwanso cha zolembedwa zokhudza mbiri ya Ufumu wa Aroma, zolembedwa zokhudza mbiri ya Ayuda ndi zimene anthu ophunzira za mbiri ya dziko lapansi a mtundu wachigiriki (chi Helena) analemba. Kuonjezera apa, mzinda wonse wa Yerusalemu unachitira umboni za izi. Mbiri yonse ilipo kuyambira pamene Yesu anali ndi ophunzira ake m'munda wa Getsemani kumene anaperekedwa, nagwidwa mpaka pa imfa yake pa mtanda ndi kuikidwa kwake m'manda.

Chifukwa chakuti adindo anadziwa za zimene Yesu anawuza ophunzira ake za kuuka kwake iwo anayika chisindikizo pa mandapo nayikanso asilikali a chi Roma kuti alondele. Ngakhale izi zinali chonchi pa tsiku lachitatu m'manda munapezeka pululu thupi la Yesu mulibemo. Izi zalembedwa bwino ku Mateyu:

*Ndipo onani panali chivomezi chachikulu pakuti mngelo wa Ambuye anatsika kumwamba nafika kukunkhuniza mwalawo, nakhala pamwamba pake. Kuoneka kwake kunali ngati mphenzi ndi chovala chake choyeretsa ngati matalala. Ndipo ndi kuopsya kwake alondawo ananthunthumira nakhala ngati anthu akufa. (Mateyu 28.2-4)*

Adindo anapeka nkhani yawo pofuna kofotokozera za kusapezeka kwa thupi la Yesu limene lidayikidwa m'manda:

*... Ndipo pamene iwo anali kupita onani alonda anafika ku mzinda nauza a nsembe aakulu zonse zimene zinachitidwa. Ndipo pamene ansonkhana pamodzi ndi akulu anakhala upo napatsa asilikaliwo ndalama zambiri nati, kazinenani kuti ophunzira ake anadza usiku namuba uja ife tikali mtulo. Ndipo ngati ichi chidzamveka kwa kazembe ife tidzamgwetsa mtima ndipo inu mudzakhala opanda nkhawa. Ndipo iwo analandila ndalamazo nachita monga anawalangiza, ndipo mbiri iyo inabuka mwa Ayuda kufikira lero lomwe. (Mateyu 28.11-15)*

**Angelo analengeza za kukwa kwa Yesu kwa akufa:**
*Koma tsiku loyamba la sabata, m'bandakucha, anadza kumanda atatenga zonunkhira adazikonza. Ndipo anapeza mwala unakunkhunizidwa kuuchotsa pa manda. Ndipo mmene analowa sanapeze mtembo wa Ambuye Yesu. Ndipo kunali mmene anathedwa nzeru nacho, taonani amuna awiri anaimilira pafupi pao atavala zonyezimira; ndipo mmene anakhala ndi mantha naweramira pansi nkhope zawo, anati kwa iwo, Mufuniranji munthu wamoyo pakati pa anthu akufa? Palibe kuno iye, komatu anauka; Kumbukurani mmene adalankhula nanu pamene analinso mu Galileya ndi kunena kuti, Mwana wa Munthu ayenera kuperekedwa mmanja mwa anthu ochimwa ndi kupachikidwa pa mtanda, ndi kuuka tsiku lachitatu'." (Luka 24.1-7)*

Posakhalitsa Yesu anaonekera kwa ophunzira ake, poyamba azimayi amene anapita ku manda ake ndipo kenako kwa akuphunzira ake:
*Pamenepo pokhala madzulo tsiku lomwelo loyamba la sabata makomo ali chitsekere, kumene anakhala ophunzira chifukwa chakuopa Ayuda, Yesu anadza naimilira pakati pao nanena nao, Mtendere ukhale ndi inu. Ndipo pamene adanena ichi anaonetsa manja ake ndi nthiti zake. Pamenepo ophunzira anakondwera pakuona Ambuye. (Yohane 20.19-20)*

M'modzi wa ophunzira ake, Tomasi, amene sanalipo pa nthawiyi ananena mopanda chikhulupiliro motere:
*"Koma ndikapanda kuona m'manja ake chizindikiro cha misomaliyo, ndi kuika chala change m'chizindikiro cha misomaliyo ndi kuika dzanja langa kunthiti yake, sindidzakhulupilira." (Yohane 20.25)*

Patatha Sabata imodzi, pamene Yesu anawonekera kwa akuphunzira, anatembenukira kwa Tomasi nati:

*"Bwera nacho chala chako kuno nuone manja anga; ndipo bwera nalo dzanja lako nuliike ku nthiti yanga, ndipo usakhale wosakhulupilira koma wokhulupilira." (Yohane 20.27)*

Patapita kanthawi kuchokera pa chiukitso, Petro analalikila mu Yerusalemu ndi kuti:

*"Amuna inu a Israeli, mverani mawu awa: Yesu mNazarayo, mwamuna wochokera kwa Mulungu, wosonyezedwa kwa inu ndi zimphamvu, ndi zozizwa, ndi zizizndikiro, zimene Mulungu anazichita mwa iye pakati pa inu monga mudziwa nokha; ameneyo woperekedwa ndi uphungu woikidwa ndi kudziwikiratu kwa Mulungu inu mwampachika ndi kumupha ndi manja a anthu osaweruzika…Yesu ameneyo Mulungu anamuukitsa za ichi tili mboni ife tonse. (Machitidwe 2.22-23, 32)*

Panalibe chikaiko pakati pa ophunzira kuti Yesu anamwaliradi ndipo kuti iwo tsopano anamuona wamoyo. Petro analemba mu kalata wake wina: *Pakuti Khristunso adamva zowawa chifukwa cha machimo, wolungama mmalo mwa osalungama, kuti akatifikitse kwa Mulungu. Wophedwatu mthupi koma wopatsidwa moyo mumzimu. (1 Petro 3.18)*

*Amene anasenza machimo athu mwini yekhayo mthupi mwake pamtanda kuti ife titafa ku machimo tikakhale ndi moyo kutsata chilungamo; ameneyo mikwingwirima yake munachiritsidwa nayo… (1 Petro 2.24)*

Kwa masiku okwanira 40, Yesu anaonekera kwa ophunzira ake ndi anthu enanso mu nthawi zosiyanasiyana:

*Pomwepo anaonekera panthawi imodzi kwa abale oposa mazana asanu amene ochuluka a iwo akhala kufikira tsopano koma ena agon. (1 Akorinto 15.6)*

Ndipo ambiri analipo ndipo anamuona pa tsiku lakukwera kwake kunka kumwamba:

*Ndipo mmene adanena izi, ali chipenyere iwo, ananyamulidwa; ndipo mtambo unamulandira iye kumuchotsa kumaso kwao. Ndipo pakukhala iwo chipenyerere kumwamba pomuka iye, taonani amuna awiri ovala zoyera anaimilira pambali pao amenso anati Amuna a ku Galileya muimiliranji ndi kuyang'ana ku mwamba? Yesu amene walandilidwa kunka ku mwamba kuchokera kwa inu adzadza momwemo monga munamuona alinkupita kumwamba." (Machitidwe 1.9-11)*

Tsono popeza ophunzira adamuona Yesu alinso wamoyo anasiya kuchita mantha ndipo analimbikitsidwa ndi chimene chidachitika. Tikhoza kunena motsindika kuti ophunzirawa sakadaika miyoyo yawo pachiswe polalikira Uthenga umene adani oti nkuwapha anali ambiri akadakhala kuti pena pake anali ndi chikaiko za kuukitsidwa kwa Yesu. Chimodzimodzinso, sakadangopeka nkhani yomati Yesu wauka ndipo oyamba kumuona ndi kudziwa za izi anali azimayi, popeza nthawi imeneyo umboni wa azimayi sumaloledwa kukhala woyenera.

**Kuonjezera pa Chipangano Chatsopano cha Baibulo, palinso mabuku ena a mbiri yakale ya dziko lapansi amene analemba za imfa ya Yesu, monga:**

Bukhu lotchedwa <u>*The Annals*</u> *(Bukhu 15, mutu 44)* lorembedwa mu chaka cha 116 AD ndi kachenjede wodziwa kulemba mbiri komanso amene anali phungu wanyumba ya malamulo nthawi ya ulamuliro wa Aroma, dzina lake Tacitus. Iyeyu analemba za kuti kupachikidwa kwa Yesu pa mtanda kunali potsatira chigamulo cha Pilato.

Bukhu lotchedwa <u>*The Antiquities of the Jews*</u> *(Bukhu 18, mutu 3.3*) lolembedwa ndi katakwe wolemba mbiri ya Ayuda wotchedwa Josephus, nalonso limafotokoza za imfa ya pa mtanda ya Yesu mu nthawi ya ulamuliro wa Pilato.

Anthu enanso olemba mbiri yakale yadziko lapansi, maka a mtundu wa Chigiriki monga *Thallus* ndi *Phlegon* wa ku Tralles analembanso

zokhudza mdima udagwa padziko kwa maola atatu pa nthawi yakupachikidwa kwa Yesu, zimene anati zinakwaniritsa ulosi wa mneneri Amosi wa mu Chipangano Chakale :

*"Ndidzasanduliza zikondwerero zanu zikhale maliro, ndi nyimbo zanu zikhale za maliro, ndi kufikitsa ziguduli mchuuno monse ndi mpala pa mutu uliwonse…nadzakhala ngati maliro a mwana mmodzi yekha ndi chitsiliziro chake ngati tsiku lowawa. (Amosi 8.9-10)*

***Nkhani ya sanda ya ku Turin m'dziko la Italy*** *6), 7)* imalimbikitsa zolembedwa mu mabuku a Uthenga wabwino amene amafotokoza za zimene zinachitika atamutsitsa Yesu pa Mtanda. Yosefe wa ku Arimathea, mkulu wa bwalo lalikulu, anapempha Pilato kuti ampatse thupi la Yesu kuti aliyike m'manda, Iye analikulunga mu nsaru naliyika m'manda osemedwa anali pafupi. *(Onani Mateyu 27.57-60; Marko 15.42-46; Luka 23.50-53; Yohane 19.38-42)*. Mabuku onse anayiwa amati ngakhale thupi la Yesu munalibe m'manda, koma nsaru zokha zinalipobe. *(Onani Luka 24.12; Yohane 20.1-8)*. Anthu amakhulupilira kuti Sanda ya ku Turin ndi nsaru imeneyi yomwe thupi la Yesu linakulungidwamo. Anthu ambiri a sayansi ayipima nsaruyi ndipo akaijambula ndi makina osiyanasiyana nsaruyi imaonetsa madindo a thupi la maliseche limene lidapachikidwa pa mtanda. Zithunzizo zimaonetsa magazi othimbilira pa nsaruyi kumene kuli manja ndi mapazi ndi mu nthiti ngakhalenso kumutu komwe kunali chisoti cha minga. Nkhope imaonekanso mu zithunzi zina. Sipaoneka fupa lothyoka pa zithunzizo.

Malingana ndi dongosolo la masiku amenewo, anthu onse opachidwa pa mtanda amawatsirizitsa powathyola miyendo kuti afe msanga komanso ndi ululu koma izi sizinachitike ndi thupi la Yesu:

*Koma pofika kwa Yesu mmene anamuona iye kuti wafa kale sanathyola miyendo yake; koma mmodzi wa asilikali anamgwaza ndi nthungo m'nthiti yake ndipo panatuluka pomwepo mwazi ndi madzi…pakuti izi zinachitika kuti lembo likwaniridwe; "fupa la iye silidzathyoledwa." Ndipo linenanso lembo lina "Adzayang'ana pa iye anampyoza." (Yohane 19.33-37)*

Akatswiri ambiri a masiku ano amanena kuti zoti Yesu anafa, zinachitikadi ndipo zoti anauka kwa akufa ndi mbiri yoona potengera ndi umboni ulipo komanso kusintha kwakukulu pa ophunzira ake chifukwa cha chiukitsochi.

**Tsono nawa mayankho a funso lakuti, Kodi Yesu Anafadi pa Mtanda?**

| **Baibulo Chipangano Chakale Inde** | **Baibulo Chipangano Chatsopano Inde** | **Mabuku ena akale Inde** | **Koran Ayi Inde – kuti anafa** |
|---|---|---|---|
| Aneneri ambiri analosela za imfa ya Mesiya: *Yesaya (Mutu 53)* *Davide (Masalmo 22)* *Amosi (8.9-10)* *Zekariah (12.10)* | Anthu ambiri anachitira umboni za imfayi mpaka ola lotsiriza ndipo anamuona ndi kumva mau ake akuthatha ndi imfa: *Mateyu 27.1-66* *Marko 15.1-41* *Luka 22.47-23.56* *Yohane 18.1-19.42* | Umboni wopezeka mu zolembedwa za mzaka za pakati pa 100 ndi 200 zimene olemba mbiri ya dziko lapansi analemba: *Tacitus, Josephus, Lucian, The Babylonian Talmud* | Ayi: Yesu sanafe pa mtanda: *Koran 4.157-158* Inde: <u>Ikuonetsa kuti Yesu adzafa:</u> *Koran 19.30-31 Koran 19.33* <u>Ikutsimikiza kuti anafadi:</u> *Koran 3.55* *Koran 5.117* *Koran 3.144* |

# *Mutu 3:*

# Kodi Yesu ndi Mwana Wa Mulungu?

Koran ndi Baibulo sizigwirizana pankhani ya kuti Kodi Yesu ndi mwana wa Mulungu.

**Koran imanena momveka bwino kuti Yesu ndi mneneri komanso Mesiya ndipo kuti kubadwa kwake kunali kwa chifuniro cha Mulungu yekha osati munthu. Komabe siyivomereza kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu:**

*Ndipo mtcule, Maryam mbukhu ili, pamene anadzipatula ku anthu aku banja lake (ndikunka) ku malo a mbali ya ku mmawa. Ndipo adadzitsekereza kwa iwo (kuti athe kutumikira Mulungu mokwanira). Ho tidatuma mngelo wathu [Gabrieli], kwa iye ndipo adadzifanizila monga munthu weniweni. Maryam adati "Ndithu, Ndikudzitchinjiriza ndi Mulungu mwini chifundo chambiri, kwa iwe ngati umawopa Mulungu. (Mngelo) adati, "Ndithu ine ndine mtumiki wa Mbuye wako (ndadza) kuti ndikupatse mwana woyera." adati, "Ndingakhale bwanji ndi mwana pomwe sadandikhudze wamuna (aliyense) ndipo ine sindili (mkazi) wachiwerewere?" (Mngelo) adati, "Ndimomwemo Mbuye wako akuti zimenezi kwa iye nzosavuta. Ndipo timchita kukhala chozizwitsa kwa anthu ndi mtendere wochokera kwa ife (Nchifukwa chake tachita izi)*

*ndipo ichi ndi chinthu chomwe chidalamulidwa kale. (chichitika monga momwe Mulungu adafunira)." (Koran 19.16-21)*

*Ndithudi, fanizo la Yesu kwa Mulungu liri ngatii fanizo la Adamu. Adamulenga ndi dothi; namuuza iye, "khala munthu," ndipo adakhala. (Koran 3.59)*

*Sikoyenera kwa Mulungu kudzipangila mwana; Iye (Mulungu) wapatukana ndi zimenezi. ndiwokwezedwa pamwamba! Akafuna chinthu amangonena kwa chinthucho "chitika" ndipo icho chimachitikadi. (Koran 19.35)*

*Ndipo (osakhulupilira omwe ndi Ayuda ndi Akhristu) akuti, "(Mulungu) mwini chifundo Chambiri wadzipangira mwana!" Ndithu mwadza ndi chinthu choipitsitsa kwambiri (pa zimene mukunenazi). Thambo layandikila kusweka ndi nthaka kuphwasuka ndi mapiri kugwa ndikudukaduka. Chifukwa cha kumunamizila (Mulungu) mwini chifundo chambiri kuti ali ndi mwana. Ndipo nkosayenera (Mulungu) mwini chifundo chambiri kudzipangira mwana. (Koran 19.88-92)*

*[Iye ndiye] mlengi wa nthaka ndi thambo zingatheke bwanji kukhala ndi mwana pomwe iye alibe mkazi? kumwamba ndi dziko lapansi. Tsono anagakhale bwanji ndi mwana pamene alibe mkazi ndipo iye analenga zinthu zonse?... (Koran 6.101)*

*…Ndipo Akhristu akuti, "Mesiya (Yesu) ndi Mwana wa Mulungu." Awo ndi mawu amene akunena ndi pakamwa pawo (opanda umboni wa Mulungu); akutsanzira za omwe sadakhulupilire kale. Mulungu awawononge; kodi iwo akusokera chotani kusiya choondi? (Koran 9.30)*

*Akunena, "Mulungu wadzipangira mwana." Wapatukana ndi zimenezo. Iye ngokwanira (salakala mwana kapena mthangati aliyense) ndi zake za kumwamba ndi dziko lapansi. Inu mulibe mboni pa zimenezi. Kodi mukumnenera Mulungu zomwe simukuzidziwa? (Koran 10.68)*

*Ndikuti liwachenjeze iwo akunena kuti, "Mulungu wadzipangira mwana." Iwo pa bodza lawolo alibe kuzindikila chinthu chili chonse cha nzeru ngakhale makolo awo. Lakula kwabasi liwu likutuluka mkamwa mwawo. Sanena china koma bodza basi. (Koran 18.4-5)*

**Koma Baibulo mbali yake liri ndi mavesi ambiri onena zakuti Yesu ndi mwana wa Mulungu.**

**Maulosi a mu Chipangano Chakale:**

*Ndidzauza za chitsimikizo, Yehovah ananena ndi ine, "Iwe ndiwe Mwana wanga ine lero ndakubala." (Masalmo. 2.7)*

*Mpsyopsyoneni mwanayo... Odala onse akumkhulupilira iye. (Masalmo 2.12)*

*"Ndipo ndidzatsanulira pa nyumba ya Davide ndi pa okhala mu Yerusalemu, mzimu wa chisomo ndi wakupembedza ndipo adzandipenyelera ine amene anandipyoza nadzamlilira monga munthu alilira mwana wake mmodzi yekha nadzamvera zowawa mmtima monga munthu amvera zowawa mwana wake woyamba." (Zekariya 12.10)*

**Mu Chipangano Chatsopano:**

*Ndipo mwezi wa chisanu ndi chimodzi, mngelo Gabriele anatumizidwa kunka ku mudzi wa ku Galileya dzina lake Nazareti, kwa namwali wopalidwa ubwenzi ndi munthu dzina lake Yosefe, wa fuko la Davide, ndipo dzina la namwali ndilo Maria. Ndipo pakulowa mngelo anati kwa iye, "Tikouneni wochitidwa chisomo, Ambuye Ali ndi iwe." Koma iye ananthunthumira ndi mau awa, nasinkhasinkha kulonjera uku nkotani. Ndipo mngelo anati kwa iye, "usaope Maria pakuti wapeza chisomo ndi Mulungu, ndipo tsono udzakhala ndi pakati nudzabala mwana wa mwamuna nudzamutcha dzina lake Yesu. Iye adzakhala wamkulu nadzatchedwa Mwana wa Wamkulukulu ndipo Ambuye Mulungu adzampatsa iye mpando wachifumu wa Davide atate wake, ndipo iye adzachita ufumu pa banja la Yakobo nthawi zonse, ndipo ufumu wake sudzatha." Koma Maria anati kwa mngelo, "ichi chidzachitika bwanji*

*popeza ine sindidziwa mwamuna?" Ndipo mngelo anayankha nati, kwa iye, "Mzimu Woyera adzafika pa iwe ndi mphamvu ya Wamkulukulu idzakuphimba iwe chifukwa chake choyeracho chikadzabadwa chidzatchedwa Mwana wa Mulungu." (Luka 1.26-35)*

*Chiyambi cha Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu Mwana wa Mulungu (Marko 1.1)*

*…Umene iye anatilonjeza kale ndi mau a aneneri ake mmalembo oyera wakunena za Mwana wake amene anabadwa mwa Mbeu ya Davide monga mwa thupi, amene anatsimikizidwa ndi mphamvu kuti ndiye Mwana wa Mulungu monga mwa Mzimu wa Chiyero ndi kuuka kwa akufa ndiye Khristu Yesu Ambuye wathu. (Aroma 1.2-4)*

*Chimene tidachiona, ndipo tidachimva tikulalikirani kuti inunso mukayanjane pamodzi ndi ife ndipo chiyanjano chathu chilinso ndi Atate ndipo ndi Mwana wake Yesu Khristu. (1 Yohane 1.3)*

*Koma ngati tiyenda mkuunika monga iye ali mkuunika tiyanjana wina ndi nzake ndipo mwazi wa Yesu Mwana wake utisambitsa kutichotsera uchimo wonse. (1 Yohane 1.7)*

*Popeza tsono tili naye wa nsembe wamkulu wopyoza miyamba, Yesu Mwana wa Mulungu tigwiritse chivomerezo chathu. (Ahebri 4.14)*

*Kale Mulungu analankhuka ndi makolo mwa aneneri mmanenedwe ambiri ndi mosiyanasiyana. Koma pakutha pake pa masiku ano analankhula ndi ife ndi mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa iyeyo analenga maiko ndi a mmwamba omwe; ameneyo pokhala ali chinyezimiro cha ulemelero wake, ndi chizindikiro chenicheni cha chikhalidwe chake, nanyamula zonse ndi mau a mphamvu yake, m'mene anachita chiyeretso cha zoipa, anakhala pa dzanja lamanja la Ukulu m'mwamba, atakhala woposa angelo monga momwe adalowa dzina lakuposa iwo. Pakuti kwa mngelo uti anati nthawi ili yonse "iwe ndiwe Mwana wanga…" (Ahebri 1.1-5)*

**Zimene Yesu Ananena:**

*“Koma Yesu anayankha iwo, Atate wanga amagwira ntchito kufikira tsopano, inenso ndigwira ntchito. Chifukwa cha ichi Ayuda anafuna kumupha, si chifukwa cha kuswa tsiku la sabata kokha komau anatchanso Mulungu Atate wake wa Iye yekha. (Yohane 5.17-18)*

*“Chifukwa chake ngati Mwana adzakuyesani inu aufulu mudzakhala mfulu ndithu.” (Yohane 8.36)*

*“Ine ndi Atate ndife amodzi.” (Yohane 10.30)*

Mafanizo a Yesu pa *Mateyu 21.33-39* ndi *Mateyu 22.1-10* akunena za iye mwini ngati Mwana ndi Atate ngati mwini malo ndi Mfumu. Mu mafanizo onsewa antchito atumidwa kukagwira ntchito, mmodzi koma onsewo anamenyedwa, kuzunzidwa ndi kuphedwa.

*“...Koma pambuyo pake anatumiza mwana wake, nati, ′Adzachitira mwana wanga ulemu′.” (Mateyu 21.37)* Ngakhale zinali choncho, pomaliza pake mwanayo anaphedwanso.

**Ziwanda (mizimu yoyipa) zimadziwa kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu:**

*Ndipo mizimu yonyansa mmene inamuona iye inamgwadira, nifuula niti, “Inu ndinu Mwana wa Mulungu.” Ndipo anailimbitsira mau kuti isamuulule. (Marko 3.11-12)*

*Marko 5.1-20* akunena za munthu amene anavutidwa ndi ziwanda ndipo kuti Yesu anamumasula munthuyo:

*Ndipo pakuona Yesu kutali anathamanga, namgwadira iye. Ndipo anafuula ndi mau olimba nanena, “ndili ndi chiani ine ndi inu, Yesu Mwana wa Mulungu Wamkulukulu? Ndikulumbilirani pa Mulungu Msandizunze!” Pakuti ananena kwa iye “tuluka iwe mzimu wonyansa kwa munthuyu!” (Marko 5.6-8)*

Pali umboni wokwanira kuti Yesu anadzitenga yekha kukhala Mwana wa Mulungu potengera m'mene amalankhulira ndi ophunzira ake:

*"Kapena uganiza kuti sindingathe kupemphera Atate wanga ndipo iye adzanditumizira tsopano lino mabungwe a angelo oposa khumi ndi awiri? Koma pakutero malembo adzakwaniridwa bwanji, pakuti kuyenera chomwecho?" (Mateyu 26.53-54)*

**Molingana ndi mau a Mulungu, Mesiya ndi Mwana wa Mulungu ndi munthu mmodzi yemweyo:**

*"Koma inu mutani kuti ine ndine yani?  Ndipo Simon Petro anayankha nati, "Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu." Ndipo Yesu anayankha iye nati, "Ndiwe wodala Simon Bara Yona pakuti thupi ndi mwazi sizinakuululira ichi koma Atate wanga wa kumwamba..." (Mateyu 16.15-17)*

*Koma Yesu anangokhala chete Ndipo mkulu wa ansembe ananena ndi iye; "ndikulumbilitsa iwe pa Mulungu wamoyo, kuti utiuze ife ngati ndiwe Khristu, Mwana wa Mulungu!" (Mateyu 26.63)*

*Koma zalembedwa izi kuti mukakhulupilire kuti Yesu ndiye Mwana wa Mulungu; ndikuti pakukhulupilira mukhale nawo moyo m'dzina lake. (Yohane 20.31)*

Pa mtanda Yesu ananyozedwa motere:

*"Anapulumutsa ena sangathe kudzipulumutsa yekha.  Ndiye Mfumu ya a Israeli, atsike tsono pa mtandapo ndipo tidzamkhulupilira iye. Amakhulupilira Mulungu iye ampulumutse ngati amfuna pakuti anati, 'Ine ndine Mwana wa Mulungu.'..." (Mateyu.27.42-43)*

Mu bukhu lomaliza la mu Baibulo, bukhu la Chibvumbulutso, Yesu akudzibvumbulutsa yekha ngati mwana wa Mulungu:

*Awa ndi mau a Mwana wa Mulungu... (Chibvumbulutso 2.18)*

**Zoti Tilingalirepo:**

Popeza mabuku onsewa a Koran ndi Baibulo amagwirizana pa zoti kubadwa kwa Yesu kunali kodabwitsa ndi kuti zinali mu chifuniro cha Mulungu osati munthu ndipo kuti mabukuwa akuvomerezana kuti iye ndiye Mesiya (Khristu), nanga zingatheke bwanji kuti munthu wotereyu angofanizidwa ndi aneneri ena onse monga akunenera mu Koran? Ichi chikutipatsa funso lakuti, kodi tikati Mesiya ndiye kuti tikutanthauza chiani?

# *Mutu 4:*

# Kodi Yesu ndi Mulungu?

**Baibulo ndi Koran zonse zimaphunzitsa kuti pali Mulungu mmodzi woyenera kupembedzedwa.**

**KORAN:**

*Ndithu iyi ndi nkhani yoona; palibe woyenera kupenmbedzedwa mwa choonadi koma Mulungu mmodzi. Ndithudi Iye Mulungu ngwamphamvu zoposa nganzeru zakuya. (Koran 3.62)*

*Ndithu Ine ndine Mulungu palibe wopembedzedwa mwa choonadi koma ine. Choncho ndipembedze, swala moyenera pondikumbukira. (Koran 20.14)*

**BAIBULO:**

Lamulo loyamba pa malamulo khumi amene Mose analandira kwa Mulungu linali loti:

*"Ine ndine Yehovah Mulungu wako amene ndinatulutsa iwe ku dziko la Ejipito, ku nyumba ya ukapolo. Usakhale nayo milungu ina koma ine ndekha..." (Eksodo 20.2-3)*

Mneneri Yesaya anati:

*...Ndipo palibenso Mulungu wina popanda ine, Mulungu wolungama ndi Mpulumutsi; palibenso wina popanda ine. (Yesaya 45.21)*

Yesu anatchulaponso malemba awa:

*Kwalembedwa: "Ambuye Mulungu wako udzamgwadira ndipo iye yekhayekha udzamlambira." (Mateyu 4.10)*

Ndipo pamene Yesu anafunsidwa kuti kodi lamulo lalikulu koposa onse ndi liti, iye anati:

*... "Mvera, Israeli: Ambuye Mulungu wathu ndiye mmodzi. Ndipo udzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse..." (Marko 12.29-30)*

**Koma tsopano Baibulo ndi Koran zimatsutsana pa za uMulungu wa Yesu, ngati mbali imodzi ya Mulungu mmodzi mwa atatu – Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera.**

**KORAN:**

*E inu anthu a buku musamalumphe malire pa chipembedzo chanu. Ndipo muamnenere Mulungu koma zowona (zokhazokha) Ndithu Mesiya mwana wa Maria ndi mtumiki wa Mulungu (ndiponso ndi munthu wolengedwa) ndi liwu lake lomwe adaliponya kwa Maria. Ndiponso ali ndi mzimu wochokera kwa Iye (Mulungu monga mizimu ina yonse imachokera kwa Iye). Choncho khulupilirani Mulungu ndi atumiki ake. Musanene "Utatu wa Mulungu" siyani (zikhulupiliro za Utatu wa Mulungu), i kutero ndi bwino kwa inu. Ndithudi Mulungu ndi Mulungu mmodzi (basi). Ulemelero wake ngotukuka kutali kukhala ndi mwana. Nzake zonse za kumwamba ndi pansi. Ndipo Mulungu ndi mtetezi wokwanira. (Koran 4.171)*

*Ndithudi am'kana Mulungu amene amanena kuti, "Mulungu ndiye Yesu mwana wa Maria." Pomwe Mesiyah adati, "Inu ana a Israeli, pembedzani Mulungu yenwe ndi mbuye wanga ndi mbuye wanu." Ndithudi amene aphatikize Mulungu ndi chinthu china, Mulungu waletsa*

*kukalowa ku manda a mtendere ndipo malo ake ndi kumoto ndipo anthu ochita zoyipa sadzakhala ndi mthandizi… (Koran 5.72)*

*Ndithudi a'mkana Mulungu amene amanena, "Mulungu ndi mmodzi mwa milungu itatu." Pomwe palibe mulungu wina koma Mulungu mmodzi… (Koran 5.73)*

*Ndipo (kumbukirani) pamene Mulungu adzanena, "Iwe Yesu, mwana wa Maria, kodi udawuza anthu kuti, 'Ndiyeseni ine ndi mayi wanga monga milungu iwiri mmalo mwa Mulungu'?" (Mneneri Yesu) adzati, "Ulemelero ukhale kwa inu, sikoyenera kwa ine kunena zomwe sizili zoyenera (kwa ine mawu amenewa ngabodza) Ngati ndikadanena ndiye kuti mukadadziwa inu. Inu mukudziwa zomwe zili mu mtima mwanga pomwe ine sindidziwa zomwe zili mwa inu… (Koran 5.116)*

*Mulungu sadadzipangile mwana ndipo palibe pamodzi ndi iye Mulungu (wina) ngati zikadakhala choncho ndiye kuti mulungu aliyense akadatenga zimene iye adalenga ndipo milungu ina ikadaipambana milungu inzawo (polimbirana ufumu. Mulungu wapatukana nazo kwambiri zimene akusimbazo. (Koran 23.91)*

*Ndipo nena, "Kutamandidwa kwabwino nka Mulungu. Yemwe sadadzipangire mwana ndipo alibe mphatikizi mu ufumu (wake) ndipo alibe mthandizi (womthandiza) nkufooka..." (Koran 17.111)*

**<u>BAIBULO:</u>**

Ngakhale kuti Baibulo limaphunzitsa za Mulungu mmodzi, limaonetsera Utatu wa Mulungu: Mulungu Atate, Mwana (Yesu) ndi Mzimu Woyera. Tiyeni tione mavesi onena za Utatu wa Mulungu mu Baibulo.

Mu nkhani ya kulengedwa kwa dziko lapansi pa mutu woyamba mu Baibulo pagwiritsidwa ntchito mau osonyeza kuchuluka kwa zinthu:

*Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m'chifanizo chathu… (Genesis 1.26)*

Mneneri Yesaya analosela za Mesiya:

*Chifukwa chake Ambuye mwini adzakupatsani inu chizindikiro: taonani namwali adzayima, nadzabala mwana wa mwamuna, nadzamutcha dzina lake Imanuele (kutanthauza Mulungu nafe). (Yesaya 7.14)*

*Anthu amene anayenda mu mdima awona kuwala kwakukulu, iwo amene anakhala m'dziko la anthu akufa kuwala kwatulukira kwa iwo…pakuti kwa ife mwana wa khanda wabadwa, kwa ife mwana wa mwamuna wapatsidwa; ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lake ndipo adzamutcha dzina lake Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu Wamphamvu, Atate Wosatha, Kalonga wa Mtendere. Zakuenjezera ulamuliro wake ndi za mtendere sizidzatha… (Yesaya 9.2, 6-7)*

*"Musaope taonani Mulungu wanu adza ndikubwezera chilango ndi kukupulumutsani…pamenepo maso a akhungu adzatsegulidwa..." (Yesaya 35.4-5)*

Mneneri Danieli anaona masomphenya a kumwamba ndipo akufotokoza za zomwe adaona:

*"Ndianaona masomphenya a usiku,*
*Taonani anadza ndi miyambo yakumwamba wina ngati Mwana wa Munthu,*
*Nafika kwa nkhalamba ya kale lomwe!*
*Ndipo anamyandikizitsa pamaso pake,*
*Ndipo anampatsa ulamuliro ndi ulemelero.*
*ndi ufumu kuti anthu onse ndi mitundu ya anthu,*
*ndi manenedwe onse, amtumikire.*
*Ulamuliro wake ndi ulamuliro wosatha,*
*Wosapitilira,*
*ndi ufumu wake*
*sudzaonongeka... (Danieli 7.13-14)*

**Mavesi ena a mu Baibulo owonotsera Umulungu wa Yesu:**

*Pa chiyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mulungu ndipo Mau ndiye Mulungu. Awa anali pachiyambi kwa Mulungu…ndipo Mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemelero wake, ulemelero wonga wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi chisomo ndi choonadi. (Yohane 1.1-2, 14)*

Utatu wonse wa Mulungu unawonekera pa ubatizo wa Yesu:

*Ndipo pamene anabatizidwa pomwepo anatuluka m'madzi; ndipo onani miyamba inatsegukira iye ndipo anapenya Mzimu wa Mulungu wakutsika ngati nkhunda nutera pa Iye; ndipo onani, mau akuchokera kumiyamba akuti, "uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa mwa iyeyu ndikondwera." (Mateyu 3.16-17)*

Nkhani imeneyi inalembedwanso pa *Marko 1.9-11* ndi *Luka 3.21-22*. Yohane M'Batizi naye anaperekera umboni za Yesu:

*Ndipo Yohane anachita umboni nati, "Ndinaona Mzimu ali kutsika kuchokera kumwamba monga nkhunda, nakhalabe pa Iye. Ndipo sindinamdziwa iye koma wonditumayo kubatiza ndi madzi, iyeyu ananena ndi ine, Amene udzaona Mzimu atsikira nakhala pa iye, yemweyu ndiye wakubatiza ndi Mzimu Woyera. Ndipo ndaona ine ndipo ndachita umboni kuti Mwana wa Mulungu ndi yemweyu." (Yohane 1.32-34)*

Mau ngati omwewa anamvekanso pamene Yesu anapita ndi ophunzira ake atatu; Petro, Yakobo ndi Yohane, ku phiri kukapemphera:

*Ndipo mkupemphera kwake, maonekedwe a nkhope yake anasandulika, ndi chovala chake chinayera ndi kunyezimira. Ndipo onani anali kulankhulana naye amuna awiri, ndiwo Mose ndi Eliya amene anaonekera mu ulemelero nanena za kumuka kwake kumene iye ati adzatsiriza ku Yerusalemu….ndipo akadalankhula izi unadza mtambo nuwaphimba iwo ndipo anaopa iwo pakulowa mu mtambo nanena, uyu ndiye Mwana wanga, wosankhidwayo; mverani iye. (Luka 9.29-31,34-35)*

Mu kalata wake wachiwiri Petro akunena za nkhani ya pa phiriyi:

*Pakuti sitinatsata miyambi yachabe, pamene tinakudziwitsani mphamvu ndi maonekedwe a Ambuye wathu Yesu Khristu koma tinapenya m'maso ukulu wake. Pakuti analandira kwa Mulungu Atate ulemu ndi ulemelero pakumdzera iye mau otere ochokera ku ulemelero waukulu, uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa, amene iye ndikondwera naye; ndipo mau awa ochokera kumwamba tidawamva ife pokhala pamodzi naye m'phiri lopatulika lija. (2 Petro 1.16-18)*

Yekha mwini adavomera kuti Iye ndiye Mesiya (Khristu) ndi Mwana wa Mulungu:

*Mkulu wa ansembe anamfunsaso ndi kuti, "Kodi iwe ndiwe Khristu, Mwana wake wa Wolemekezeka?" Ndipo Yesu anati, "ndine amene; ndipo mudzaona Mwana wa Munthu ali kukhala ku dzanja lamanja la mphamvu ndi kudza ndi mitambo yakumwamba." (Marko 14.61-62)*
Izi zikugwirizana ndi zimene Davide analemba pa Ma*salmo 110.1.*

Yesu anayimbidwa mulandu wonyoza Mulungu:

*Ayuda anatolanso miyala kuti amponye iye. Yesu anayankha iwo, ndakuonetsani inu ntchito zabwino zambiri za kwa Atate; chifukwa cha ntchito iti ya izo mundiponya miyala? Ayuda anayankha iye, "chifukwa cha ntchito yabwino sitikuponyani miyala, koma chifukwa cha mwano, ndikuti inu muli munthu mudziyesera nokha Mulungu." (Yohane 10.31-33)*

*Ayuda anamyankha iye, "Tili nacho chilamulo ife, ndipo monga mwa chilamulocho ayenera kufa chifukwa anadziyesera Mwana wa Mulungu." (Yohane 19.7)*

Tomasi wophunzira wa Yesu ananena mau awa ataona Yesu wouka kwa akufayo ali ndi moyo:

*"Ambuye wanga ndi Mulungu wanga!" Yesu ananena kwa iye, "Chifukwa wandiona ine, wakhulupilira, odala iwo akukhulupilira, angakhale sanaona." (Yohane 20.28-29)*

Paulo Mtumwi analemba kuti:

*… Mukhale nawo mtima monga unali mwa khristu Yesu, ameneyo pokhala nawo maonekedwe a Mulungu, sanachiyesa cholanda kukhala wofana ndi Mulungu, koma anadzikhuthula yekha natenga maonekedwe a kapolo nakhala mmafanizidwe a anthu ndipo popezedwa mmaonekedwe anadzichepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pa mtanda. Mwa ichinso Mulungu anamkwezetsa iye nampatsa dzina limene liposa maina onse. (Afilipi 2.5-9)*

**Yesu anafotokozera za Utatu wa Mulungu (Kulumikizika kwa Mukungu Mmodzi mwa Atatu) atangokhala pang'ono kuti amugwire:**

*"Ngati mukonda ine sungani malamulo anga. Ndipo ine ndidzapempha Atate ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe ina, kuti akhale ndi inu ku nthawi yonse, ndiye Mzimu wa Choonadi amene dziko lapansi silingathe kumlandira pakuti silimuona iye; inu mumzindikira iye; chifukwa iye akhala ndi inu nadzakhala mwa inu." (Yohane 14.15-17)*

*"Ngati wina akonda ine, adzasunga malamulo anga; ndipo Atate wanga adzamkonda, ndipo tidzadza kwa iye ndipo tidzayesa kwa iye mokhalamo." (Yohane 14.23)*

*"Izi ndalankhula nanu, pakukhala ndi inu. Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, iyeyo adzaphunzitsa inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu." (Yohane 14.25-26)*

*"Mwamva kuti ine ndinanena kwa inu, ndimuka ndipo ndidza kwa inu. Mukadandikonda ine mukadakondwera kuti ndipita kwa Atate, pakuti Atate ali wa mkulu ndi Ine." (Yohane 14.28)*

*“Koma pamene wafika Nkhoswe amene ndidzamtuma kwa inu kuchokera kwa Atate, Ndiye Mzimu wa Choonadi, amene atuluka kwa Atate, Iyeyu adzandichitira ine umboni. Ndipo inunso muchita umboni pakuti muli ndi ine kuyambira chiyambi.” (Yohane 15.26-27)*

*Koma ndinena Ine choonadi ndi inu; kuyenera kwa inu kuti ndichoke ine; pakuti ngati sindichoka, Nkhosweyo sadzadza kwa inu koma ngati ndipita ndidzamtuma kwa inu. (Yohane 16.7)*

*“Ndinatuluka kwa Atate ndipo ndadza ku dziko lapansi; ndilisiya dziko lapansi ndipo ndipita kwa Atate.” (Yohane 16.28)*

*Kulibe munthu anaona Mulungu nthawi zonse; Mwana wobadwa yekha wakukhala pa chifuwa cha Atate iyeyu anafotokozera. (Yohane 1.18)*

**Zoti tilingalirepo mozama:**

Dziwani kuti mu Koran pena paliponse pamene Allah akulankhula amagwiritsa ntchito mau oonetsa kuchuluka kwa zinthu (ife) koma mu Baibulo malo ambiri pamene Mulungu akulankhula amagwiritsa ntchito mau akuti “Ine.” Komabe monga mwa chiphunzitso cha Baibulo Mulungu ndi mmodzi mwa atatu pamene Korani imati palibe zoti Atate, Mwana ndi Mzimu. Tsono nanga m’chifukwa chiyani Korani imagwiritsa mau akuti “ife” pamene Allah akulankhula m’malo mwa mau akuti “ine?”

# *Mutu 5:*

# Kodi Yesu ndi Mpulumutsi Wa Dziko Lapansi?

**Koran imati Yesu ndi mneneri komanso Mesiya, koma simavomereza kuti Yesu ndi Mpulumutsi wadziko lapansi koma ngati mmodzi wa atumiki ena onse:**

*Mesiya, mwana wa Maria, Sali chilichonse koma ndi mtumiki wa Mulungu chabe. Ndithudi atumiki ambiri anapita kale pa tsogolo pake. Nayenso mayi wake ndi mkazi wa choonadi; onse awiri anali kudya chakudya... (Koran 5.75)*

*Nenani, "Takhulupilira Mulungu ndi zomwe zabvumbulutsidwa kwa Ibrahamu ndi Ishimaeli ndi Isihaka ndi Yakuuo ndi zidzukulu zake, ndi zimene zinapatsidwa Musa ndi Yesu ndi aneneri (ena) zochokera kwa Mbuye wawo. Sitisiyanitsa aliyense pakati pawo ndipo ife kwa iye ndi odzipereka kwa thunthu." (Koran 3.84)*

**Koma mbali inayi Baibulo limanenetsa tchutchutchu kuti Yesu ndi Mpulumutsi wa dziko lapansi ndi kuti anafa ngati nsembe yoperekedwa chifukwa cha machimo athu:**
*Koma pakusinkhasinkha iye zinthuzi onani mngelo wa Ambuye anaonekera kwa iye mkulota nanena; Yosefe, mwana wa Davide, usaope*

*kudzitengera wekha Maria mkazi wako, pakuti icho cholandiridwa mwa iye chili cha Mzimu Woyera. Ndipo adzabala mwana wa mwamuna ndipo adzamutcha dzina lake Yesu, pakuti iyeyo adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo. (Mateyu 1.20-21)*

*Ndipo panali abusa m'dziko lomwelo, okhala kubusa ndi kuyang'anira zoweta zawo usiku. Ndipo mngelo wa Ambuye anaimilira pa iwo ndi kuwala kwa Ambuye kunawaunikira kozungulira: ndipo anaopa ndi mantha akulu. Ndipo mngelo anati kwa iwo "musaope, pakuti onani ndikuuzani inu Uthenga Wabwino wa chikondwelero chachikulu chimene chidzakhala kwa anthu onse, pakuti wakubadwirani inu lero m'mudzi wa Davide, Mpulumutsi, amene ali Khristu Ambuye. Ndipo ichi chizindikiro kwa inu: mudzapeza mwana wa khanda wokuta ndi nsaru atagona modyera." (Luka 2.8-12)*

Yesu anati za iye mwini:

*…Mwana wa Munthu sanadze kutumikiridwa koma kutumikira, ndikupereka moyo wake dipo la anthu ambiri. (Mateyu 20.28)*

**Mavesi ena amati:**

*Koma iye analasidwa chifukwa cha zolakwa zathu, natunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu, chilango chotitengera ife mtendere chinamgwera iye ndipo ndi mikwingwirima yake tachiritsidwa. (Yesaya 53.5)*

*…Anachotsedwa ku chipsinjo ndi chiweruziro…pakuti walikhidwa kunja kuno chifukwa cha kulakwa kwa anthu anga. (Yesaya 53.8)*

*Iye adzaona zotsatira mavuto a moyo wake nadzakhuta nazo ndi nzeru zake mtumiki wanga wolungama adzalungamitsa ambiri. (Yesaya 53.11)*

*Koma iye mmene adapereka nsembe imodzi chifukwa cha machimo anakhala pa dzanja lamanja la Mulungu. (Ahebri 10.12)*

*Koposa kotani nanga mwazi wa Khristu amene anadzipereka yekha wopanda chilema kwa Mulungu mwa Mzimu wosatha, udzayeretsa chikumbumtima chanu kusayanitsa ndi ntchito zakufa kukatumikira Mulungu wa moyo! (Ahebri 9.14)*

*Ndipo popeza kwaikika kwa munthu kufa kamodzi ndipo atafa, chiweruziro, kotero Khristunso ataperekedwa nsembe kamodzi kukasenza machimo a ambiri adzaonekera pa nthawi yachiwiri, wopanda uchimo, kwa iwo amene amlindilira kufikira chipulumutso. (Ahebri 9.27-28)*

*M'mene adatikhululukira ife zolakwa zonse adatha kutifafanizira cha pa ifecho cholembedwa m'zoikikazo chimene chinali chotsutsana nafe, ndipo anatichotsera ife pakatipo ndikuchikhomera ichi pa mtanda. (Akolose 2.13-14)*

*Amene anatilanditsa ife ku ulamuliro wa mdima, natisunthitsa kutilowetsa mu ufumu wa Mwana wa chikondi chake amene tili nao maomboledwe mwa iye, m'kukhululukidwa kwa zochimwa zathu. (Akolose 1.13-14)*

*Pakuti kunamkomera Atate kuti mwa iye chidzalo chonse chikhalire, mwa iyenso kuyanjanitsa zinthu zonse kwa iye mwini atachita mtendere mwa mwazi wa mtanda wake, mwa iyetu kapena za padziko kapena za m'Mwamba. (Akolose 1.19-20)*

*…Ndipo yendani m'chikondi monganso Khristu anakukondani inu, nadzipereka yekha mmalo mwathu, chopereka ndi nsembe kwa Mulungu, ikhale fungo lonunkhira. (Aefeso 5.2)*

*Koma mukhalirane okoma wina ndi nzake, a mtima wachifundo, akukhululukirana nokha, monganso Mulungu mwa Khristu anakhululukira inu. (Aefeso 4.32)*

*Khristu anatiombola ku tembelero la chilamulo atakhala tembelero mmalo mwathu pakuti kwalembedwa, wotembeleredwa aliyense wopachikidwa pamtengo. (Agalatiya 3.13)*

*Ndiko kunena kuti Mulungu anali mwa Khristu alinkuyanjanitsa dziko lapansi kwa iye yekha osawerengera zolakwa zao… yanjanitsidwani ndi mulungu. Ameneyo sanadziwa uchimo anamyesera uchimo m'malo mwathu kuti ife tikhale chilungamo cha Mulungu kwa iye. (2 Akorinto 5.19-21)*

*Ndipo ife tapenya ndipo tichita umboni kuti Atate anatuma mwana akhale Mpulumutsi wadziko. (1 Yohane 4.14)*

…Kwa iye amene atikonda ife natimasula kumachimo athu ndi mwazi wake natiyesa ife Ufumu tikhale ansembe a Mulungu, ndiye Atate wake... *(Chibvumbulutso 1.5-6)*

*Ameneyu aneneri onse anamchitira umboni, kuti onse akumnkhulupilira iye adzalandira chikhulululukiro cha machimo awo, mwa dzina lake. (Machitidwe 10.43)*

**Yesu ndiye chifungulo (makiyi) cha ku chipulumutso monga mwa Baibulo:**

*Pakuti Mulungu anaconda dziko lapansi kotero kuti anapatsa mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupilira iye asatayike, koma akhale ndi moyo wosatha. Pakuti Mulungu sanatune Mwana wake ku dziko lapansi kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapilumutsidwe ndi iye. Wokhulupilira iye saweruzidwa; wosakhulupilira waweruzidwa ngakhale tsopano chifukwa sanakhulupilire dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. (Yohane 3.16-18)*

*Pakuti Uthenga Wabwino sundichititsa manyazi, pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupilira... (Aroma 1.16)*

*Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi chake cha mwini yekha m'menemo kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Khristu adatifera ife.*

*Ndipo tsono popeza tinayesedwa olungama ndi mwazi wake, makamaka ndithu tidzapulumuka mkwiyo wa Mulungu mwa iyeyo. Pakuti ngati pokhala ife adani ake, tinayanjanitsidwa ndi mulungu mwa imfa ya mwana wake, makamaka popeza ife tayanjanitsidwa, tidzapulumuka ndi moyo wake. (Aroma 5.8-10)*

*...Kuti ngati udzavomereza mkamwa mwako, Yesu ndiye Ambuye, ndikukhulupilira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa udzapulumuka. (Aroma 10.9)*

*Ndipo palibe chipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba lopatsidwa kwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo. (Machitidwe 4.12)*

*Mutu 6:*

# Kodi Yesu ndi Mkhalapakati Pa Mulungu ndi Munthu?

**Mabuku onse, Baibulo ndi Koran amati Mulungu ndi woyera, mlengi wa zonse, wamphamvu zonse, wodziwa zonse, wopezeka ponseponse nthawi ili yonse, wamuyaya ndikuti munthu sangamuyandikire potengera kuyenera kwake (kwa munthu) ayi.**

**Korani imati** munthu sangayandikire Mulungu popanda iye kumuvomereza:

*Mulungu – Palibe wopembedzedwa wina koma iye wamoyo wamuyaya, woimira ndi woteteza chilichonse. Kusinza sikumgwira ngakhale tulo. Zonse za ku mwamba ndi zapansi nza iye. Kodi ndani angathe kuombola kwa iye opanda chilolezo chake? Akudziwa zapatsogolo ndi zomwe zili pa mbuyo pawo ndipo zolengedwazo sizidziwa chilichonse pa zomwe zili nkudziwa kwake kupatula zomwe wafuna ... (Koran 2.255)*

**Baibulo limati izi zonse (zakuyandikira Mulungu) zidasintha ndi kudza kwa Yesu:**

Umboni unawonekera pamene Yesu amafa kuti chinsaru chotchinga (chikatani) cha mu kachisi chinang'ambika pakati modabwitsa kusonyeza kuti njira imene inali yobisika kwa anthu tsopano inatsegulidwa kudzera

mu imfa ya Yesu. Chotsatira chake ndi kuti timafika ndikulimbika mtima ku mpando wachifumu wa Mulungu monga akunenera pa *Ahebri 10:19-20* ndi *Ahebri 4:14-16*.

**Mabuku onse a mu Baibuilo amaonetsera, mwa njira ina yake, za Mesiya wolonjezedwayo:**
Pa Eksodo mutu 12 pali chionetsero cha Paska (mwana wa nkhosa) amene mwazi wake unapulumutsa ana a Israeli ku imfa ya mwana woyamba ndipo anatuluka ku ukapolo mu Ejipito. Mwana wa nkhosa amayenera kukhala wa mwamuna, wopanda chilema, wosathyoledwa mafupa pomudya zimene zimaonetsera Mesiya ngati mwana wa nkhosa woperekedwa nsembe.

Yohane M'batizi analandila za bvumbulutsoli ataona Yesu:
*M'mawa mwake anaona Yesu alinkudza kwa iye, nanena, Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo la dziko lapansi! (Yohane 1.29)*

Petro akuthirira ndemanga kuti:
*Podziwa kuti simunaomboledwa ndi zovunda, golide ndi siliva, kusiyana nao makhalidwe anu achabe ochokera kwa makolo anu, koma ndi mwazi wa mtengo wake wapatali monga wa mwanawankhosa wopanda chilema ndi wopanda banga, ndiwo mwazi wa Khrisru. (1 Petro 1.18-19)*
Mtumwi Yohane wophunzira wa Yesu, nayenso anaona masomphenya a ku mwamba kumene anaona Yesu ngati Mwanawankhosa wa Mulungu. *(Onani Chibvumbulutso 5.6-14; 7.9-17; 22.1-3)*

**Mabuku onse awiri Koran ndi Baibulo amakambapo kwambiri za vuto la munthu kuti ndilo tchimo koma chimene amasiyana kwambiri ndi kunena kuti ngati vutoli linakonzedwa ndi Yesu kapena ayi -**
Kuti ngati Yesu alidi amene anadzitcha yekha, kuti kodi anapachikidwadi kutitengera ife chipulumutso monga ananenera aneneri akale?

**Korani imati:**
*Uyo ndi Issa (Yesu), mwana wa Maryam – (Awa ndi) mau owona amene (Akhristu) akuwakana. (Koran 19.34)*

**Baibulo limanenetsa tchutchutchu kuti Yesu ndiye mkhala pakati pa Mulungu ndi munthu; kuti munthu sangalowe kumwamba kapena kufika kwa Mulungu popanda iyeyo:**

*Ndipo Yesu anati, "... Palibe munthu adza kwa Atate koma mwa ine. (Yohane 14.6)*

*Kuchokera komweko akhoza kupulumutsa konsekonse iwo akuyandikira kwa Mulungu popeza ali nawo moyo wake chikhalire wakuwapemnbedzera iwo…pakuti ichi anachita kamodzi kwatha, podzipereka yekha. (Ahebri 7.25, 27)*

*Ndipo mwa ichi ali nkhoswe ya Chipangano Chatsopano, kotero kuti popeza kudachitika imfa ya kuombola zolakwa za pa chipangano choyamba, oitanidwawo akalandire lonjezano la zolowa zosatha. (Ahebri 9.15)*

*Pakuti onse amene anamulandila iye ndi kukhulupilira pa dzina lake, anawapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu– (Yohane 1.12)*

Saulo wa ku Tariso anadzipereka kufuna kuthetsa chiyambi cha mpingo (Chikhristu), pozunza Akhristu kufikira tsiku lina ali pa njira kunka ku Damasiko kumene iye amapita kuti akagwire Akhristu ndikuwabweretsa ku ndende ya ku Yerusalemu, Yesu anamuimitsa. Nkhaniyi tikuipeza pa *Machitidwe 9.1-19,* ndipo ulendo umenewu unasintha kwathunthu moyo wa Saulo amene anakhala wophunzira wa Khristu komatu wachangu:

*Ndipo poyenda ulendo wake kunali kuti iye anayandikira Damasiko ndipo mwadzidzidzi kunawala momzingira kuunika kochokera kumwamba; ndipo anagwa pansi, namva mau akunena naye, "Saulo, Saulo undilondalonderanji?" Koma nati "ndinu yani Mbuye?" Ndipo anati, "ndine Yesu amene umlondalonda." (Machitidwe 9.3-5)*

Munthu yemweyu, Saoulo, amene anatchedwa Mtumwi Paulo atatembenuka mtima analemba makalata ambiri mu Chipangano Chatsopano. Tiyeni tilaweko zina za zolemba zake:

*Mauwa ali okhulupirika ndi oyenera konse kuti awalandire, kuti Yesu Khristu anadza ku dziko lapansi kupulumutsa ochimwa; wa iwowa ine ndine woposa. (1 Timoteo 1.15)*

*Pakuti ichi nchokoma ndi cholandilika pamaso pa Mulungu Mpulumutsi wathu amene afuna anthu onse apulumuke nafike pozindikira choonadi. Pakuti pali Mulungu mmodzi ndi mtetezi mmodzi pakati pa Mulungu ndi anthu ndiye munthu, Khristu Yesu, amene anadzipereka yekha chiombolo mmalo mwa onse, umboni mnyengo zake. (1 Timoteo 2.3-6)*

*Tili ndi maomboledwe mwa mwazi wake chikhululukiro cha zochimwa... (Aefeso 1.7)*

Baibulo limati anthu onse ndi ochimwa ndi kuti machimo anthu ayenera kukhululukidwa ndi kutsukidwa kuti ife tikalowe kumwamba:
*…Pakuti onse anachimwa naperewera pa ulemelero wa Mulungu ndipo ayesedwa olungama kwa ulere ndi chisomo chake mwa chiombolo cha mwa Khristu Yesu amene Mulungu anamuika poyera akhale chotetezera mwa chikhulupiliro cha m'mwazi wake, kuti aonetse chilungamo chake… (Aroma 3.23-25)*

*Pakuti mphotho ya uchimo ndiyo imfa, koma mphatso ya ulele ya Mulungu ndiyo moyo wosatha mwa Khristu Yesu Ambuye wathu. (Aroma 6.23)*

**Zoyenera Kulingalirapo Mozama:**

Korani ndi Baibulo zonse zimaphunzitsa kuti mwa munthu muli mzimu umene umakhalabe ngakhale munthuyo amwalira ndikuti munthu adzaweruzidwa ndi Mulungu kuti awone ngati ali woyenera kulowa mu paradizo (kumwamba) kapena kupita ku Gehena (moto wosatha).

Mabuku onsewa, Baibulo ndi Koran amalimbikitsa kuchita ntchito zabwino. Komabe ngakhale izi zili choncho, Baibulo limaphunzitsa kuti ntchito zabwino pazokha sizingamutengere munthu chipulumutso popeza sizingafafanize machimo athu. *(Onani Ahebri 9.22)*

Baibulo limati Mulungu anatumiza mwana wake yekhayo Yesu kuchokera m'chikondi chake kuti ife tikhale ndi moyo wosatha ndi mulungu. Tikapanda kuvomereza Yesu ngati Mpulumutsi wathu ndiye kuti tatayika kwa muyaya. *(Onani Yohane 3.16)*

**Ndi chifukwa chake funso lakuti Kodi yesu ndi ndani liri lofunika kwambiri.**

*Mutu 7:*

# Kudalilika Kwa Mabuku Awiriwa

Ngakhale kuti Baibulo ndi Koran zimagwirizana mu nkhani zina, kusiyana kwao ndi kwakukulu chifukwa amasiyana kwathunthu mu mfundo zikuluzikulu zofunika. Ichi chimapangitsa munthu kuti afunse funso lakuti: **Kodi Choonadi ndi Chiyani?**

Fundo zikuluzikulu zimene Baibulo siligwirizana ndi Koran ndi zakuti Kodi Yesu ndi Mwana wa Mulungu? Nanga kodi anapachikidwadi pa mtanda ndi kufa? Izi ndi mfundo zikuluzikulu.

Kuti munthu apeze choonadi ndiye kuti ayenera kutsegula malingaliro ake ndi mtima wake; ayenera kukonzeka kuyamba ulendo wofufuza ndipo kuti alolere kutenga zimene akuzipeza kuti ndi choonadi. **Funso ili ndi lofunika kwambiri: Kodi choonadi chenicheni cha Yesu ndi Chiti?** Kodi takonzeka kupeza mayankho ake? Chifukwatu mayankhowo akhoza kusinthiratu miyoyo yathu kwa muyaya.

**<u>Kudalilika kwa Koran ndi Baibulo:</u>**

Tiyeni tifananize mabuku awiriwa:

**Koran** inabwera ndi Mneneri Muhammad amene analandila uthengawu kudzera mwa mngelo.

**Baibulo** linalembedwa ndi aneneri, mafumu, oweruza, ophunzira a Yesu, azichimwene ake awiri a Yesu, dokotala wa chipatala ndi anthu ena owopa Mulungu. Mulungu anayenda ndi kulankhula ndi ena a iwo, angelo anawonekera kwa ambiri ndipo onsewa anali odzazidwa ndi Mzimu wa Mulungu. *(Onani 2 Timoteo 3.16)*

Ena analemba zimene adaziona ndi maso awo. Ena analemba mauthenga ochokera kwa Yehovah, ngati ndakayulo za ma pemphero ndi malambiro, mau a nzeru, maulosi ndi masomphenya amene Mulungu adawaonetsera.

**M'dandanda wofananiza kudalilika kwa Baibulo ndi Koran**

| **Mitu Yofananizidwa** | **Baibulo** | **Koran** |
|---|---|---|
| Yesu – Mwana wa Mulungu | Inde | Ayi |
| Yesu – Anafera pa mtanda | Inde | Ayi |
| Mauneneri olembedwa okhudza Mesiya | Oposa 300 alipo. Olembedwa zaka zambiri Yesu asanabadwe | |
| Mauthenga a angelo onena za Yesu | Mngelo anamuuza Maria kuti adzabala mwana wa mwamuna adzatchedwa Mwana wa Mulungu. *(Onani Luka 1.30-35)* Mngelo anaonekera kwa Yosefe kumuuza kuti Maria adzabala mwana wamwamuna amene adzapulumutsa anthu ake ku machimo. *(Onani Mateyu 1.20-21)* Mngelo anaonekera kwa abusa a ng'ombe ku Betelehemu kuwauza kuti wakubadwirani Mpulumutsi (Mesiya). *(Onani Luka 2.8-11)* | Mngelo anaonekera kwa Maria kumuuza kuti adzabala mwana wa mwamuna adzatchedwa Mesiya. *(Onani Koran 3.45)* Mngelo anaonekera kwa mtumiki Muhammad kumuuza kuti Yesu sindiye Mwana wa Mulungu. *(Onani Koran 4.171; 6.101; 9.30)* |

| | | |
|---|---|---|
| Amene anakhala, kuyenda ndi kumuona Yesu ndipo iwo anavomereza kuti Yesu analidi Mwana wa Mulungu | Yohane M'batizi, Ophunzira a Yesu (Petro, Yakobo, Yohane) – onse awa anayi anamva mau ochokera kumwamba kunena kuti yesu ndi Mwana wanga Wokondedwa koma ophunzira atatuwa anaonanso Yesu akusandulika mu ulemelero. *(Onani Mateyu 3.13-17; Luka 9.28-35)* | |
| Amene anaona Yesu Akupachikidwa pa Mtanda | Oyima pansi pa Mtanda:<br>Yohane wophunzira, Maria amake a Yesu, M'bale wa Maria, Maria mkazi wa Cleopa, ndi Maria Magadalena. *(Onani Yohane 19.25)*<br><br>Oima Pakatali:<br>Khamu limene lidamudziwa kuphatikizapo akazi amene adamulondola kuchokera ku Galileya wapansi. *(Onani Luka 23.49)* | |
| Anthu amene anaona ndi kuchitira umboni za kuuka kwa Yesu kwa akufa | Angelo awiri anaonekera kwa Maria Magadalena ndi ophunzira ake kuwauza kuti iye wauka. *(Onani Luka 24.1-8)*<br>Saulo wa ku Tariso ndi unyinji wochuluka anamuona Yesu atauka kwa akufa. *(Onani Yohane 20.10-31; Machitidwe 9.3-7; 1 Akorinto 15.6-7)* | |

| | | |
|---|---|---|
| Sanda ya ku Turin m’dziko la Italy | Amakhulupilira kuti ndi nsaru imane anakulungira thupi la Yesu poliyika m’manda ndipo kuti ndi imene inatsalira m’mandamo iye atauka kwa akufa. Mabuku onse anayi a Uthenga Wabwino anakamba za nsaruyi. | |
| Kutalika Kwa Nthawi: Kuyambira pamene zidachitika kufikira pamene zimakalembedwa ngati bukhu | Chipangano Chatsopano chinalembedwe pakati pa zaka 40 ndi 100 AD.* Mabuku a Uthenga wabwino analembedwa pakati pa zaka 60 ndi 95 AD ndipo analembedwa ndi anthu osiyana koma mosatsutsana. Nkhani ya kupachikidwa ndi imfa ya Yesu inalembedwa mwatsatanetsatane ndi anthu adaziona. Marko analemba bukhu lake patangopita zaka 30 chipachikidwireni Yesu, pamene kalata woyamba wa Paulo analembedwa mu chaka cha 50 AD, patangotha zaka 20 chiphedwereni Yesu. Apa ndekuti zambiri zidali zisadaiwalike komanso mboni zambiri zikadali moyo. Izi zimapangitsa kudalilika kwa umboniwo. | Koran inalembedwa mu zaka za 610 mpaka 632 AD, patatha zaka 600 chipachikidwireni Yesu, kuuka ndi kukwera kwake kumwamba. |

| | | |
|---|---|---|
| Kusungika kwa Mabuku enieni oyambawo | Bukhu lenileni lakale la Chipangano Chatsopano limene lidapezeka ndi limene ankagwiritsa ntchito mu chaka cha 130 AD. Mabuku ena oposa 24.000 a Chipangano Chatsopano alipo ndipo onsewo zolemba zawo sizosiyana. Izi zikusonyeza kuti Baibulo silinasinthidwe. | Mabuku akale a Korani ndi a zaka za pafupi ndi nthawi imene analembera. Zikusonyeza kuti mau a mu Koran sanasungunulidwe. |
| Mabukhu amene anapezeka ku Nyanja ya kuchidikha (Dead Sea) ku Israel *8)* mu zaka za 1946, 1947 ndi 1956 | Mabukuwa ali ndi Chipangano Chakale chonse kupatula Estere ndi Nehemia. Buku lonse la Yesaya liripo. Mabukuwa ndi azaka zoposa 2000 ndipo amafanana kwathuthu zolemba zake ndi Baibulo lamakono kusonyeza kuti zoti Baibulo linasinthidwa ndi bodza. | |
| Kulunjika kwa nkhani za mu Baibulo | Maulosi ambiri a mu Baibulo anakwaniritsidwa ena akukwaniritsidwabe. Maina a anthu ndi mizinda yambiri yomwe ili mu Baibulo anapezeka kuti ndionadi pochita kafukufuku wa mbiri yakale (histoy). Mbiri ya Baibulo imagwirizana ndi mbiri za maiko ena pa zimene zidachitika. Mafumu, nkhondo, chikhalidwe ndi zina zambiri zimene Baibulo limanena ndi zochitikadi. | |

* AD (Anno Domini = Mau a chi Latini kutanthauza kuti Chibadwireni Yesu).

## Mau Omaliza

Tiyeni timalize kufananizaku ndi mau ochokera mu Koran:

*Nena, (kwa omphatikiza Mulungu ndi mafano) "zikadakhala kuti (Mulungu) wa Chifundo chambiri ali ndi mwana, ndiye kuti ine ndikadakhala woyamba kumpembedza (mwanayo chifukwa chakuti ndi mwana wa Mulungu)." (Koran 43.81)*

Mau awa akunena choonadi kuti ngati ife timuona Yesu kuti ndiye Mwana wa Mulungu, ndiye kuti iye ndiwoyenera kulambiridwa.

Yesu anati:

*"Idzani kwa ine inu nonse akulema ndi kuthodwa ndipo ine ndidzakupunulitsani." (Mateyu 11.28)*

*"Ndipo onani ine ndili pamodzi ndi inu kufikira chimaliziro cha nthawi ya pansi pano." (Mateyu 28.20)*

**Molingana ndi zimene Koran imanena komanso zimene Baibulo likunena, Mau a Yesu ndi oyenera kuwakhulupilira:**
*Uyo ndi Issa (Yesu), mwana wa Maryam, mau owona… (Koran 19.34)*

*Yesu anayankha, "… Ndinabadwira ichi ine ndipo ndinadzera ichi kudza ku dziko lapansi kuti ndikachite umboni ndi choonadi. Yense wakukhala mwa choonadi amva mau anga." (Yohane 18.37)*

Ngati inu wokondedwa mwawerenga bukhuli mosamalitsa, ndikhulupilira kuti tsopano mkati mwa mtima wanu kuti Yesu ndi ndani ndi kuti choonadi chimecho chikutanthauza chiyani pa moyo wanu.

Ngati mufuna kudziwa zambiri za munthu wodabwitsayu Yesu, mukhoza kuwerenga mabukhu a Uthenga Wabwino mu Chipangano Chatsopano cha Baibulo.

## Maina A Yesu Mu Koran ndi Mu Baibulo

**Mu Koran:**

Isa / Yesu *(Koran 3.45)*
Mesiya *(Koran 3.45)*
Mwana wa Maria *(Koran 19.34)*
Mau a Choonadi *(Koran 19.34)*

**Mu Baibulo:**

Immanuel *(Yesaya 7.14)*
Yesu Khristu (Yeshua Mesiya) *(Machitidwe 4.10)*
Yesu wa ku Nazareti *(Luka 24.19)*
Mwana wa Mpala matabwa *(Mateyu 13.55)*
Mwana wa Munthu *(Mateyu 25.31)*
Mwana wa Mulungu *(Mateyu 3.11)*
Mfumu ya Ayuda *(Mateyu 27.37)*
Wauphungu Wodabwitsa *(Yesaya 9.6)*
Mulungu Wamphamvu *(Yesaya 9.6)*
Tate Wamuyaya *(Yesaya 9.6)*
Kalonga wa Mtendere *(Yesaya 9.6)*
Mwanawankhosa wa Mulungu (*Yohane 1.29)*
Mkango wa Yuda *(Chibvumbulutso. 5.5)*
*Wokhulupirika ndi Woona (Chibvumbulutso 19:11)*
Mau a Mulungu *(Chibvumbulutso 19.13)*
Ambuye Yesu Khristu *(Akolose 1.3)*
MFUMU YA MAFUMU NDI MBUYE WA AMBUYE *(Chibvumbulutso. 19.16)*

## Ziphunzitso Zina Za Yesu

*Ndipo ndichilitsa osapenya [Chibadwire] ndi wamaangamaanga ndikuukitsa wakufa… (Koran 3.49)*

*Koma ine ndinena kwa inu kondanani nao adani anu ndikupempherera iwo akuzunza inu. (Mateyu 5.44)*

*Chifukwa chake zinthu zili zonse mukafuna kuti anthu achitire inu, inunso muwachitire iwo zotero; pakuti icho ndicho chilamulo ndi aneneri. (Mateyu 7.12)*

*Koma inu pamene mupemphera munene:*
*Atate wathu wakumwamba,*
*Dzina lanu liyeretsedwe.*
*Ufumu wanu udze.*
*Kufuna kwanu kuchitidwe*
*Monga kumwamba chomwecho pansi pano.*
*Mutipatse ife lero chakudya chathu cha lero.*
*Ndipo mutikhululukire mangawa athu,*
*Monga ifenso tawakhululukira amangawa athu.*
*Ndipo musatitengere kokatiyesa,*
*Koma mutipilumutse kwa woipayo.*
*Pakuti wanu ndi ufumu ndi mphamvu ndi ulemelero ku nthawi za nthawi.*
*Amen. (Mateyu 6.9-13)*

# Mabuku Amene Anagwiritsidwa Ntchito Pa Kafukufuku

1) Lucian of Samosata. (165). *The Passing of Peregrinus (The Death of Peregrinus)*. (11-13).
English Translation: A.M. Harmon. (1936). (Vol. 5, p.12-15). Loeb Classical Library edition.
https://earlychurchtexts.com/public/lucian_passing_of_peregrinus.htm

2) *The Babylonian Talmud.* (70-200). English Translation: I. Epstein. (London: Soncino, 1935). Vol. III, Sanhedrin 43a, 281, cited in Habermas. The Historical Jesus, 203.
https://www.bethinking.org/jesus/ancient-evidence-for-jesus-from-non-christian-sources

3) Josephus, Flavius. (93). *Antiquities of the Jews* (*Book 18*, chapter 3.3)
English Translation: William Whiston. (1737)
https://archive.org/details/completeworksofj03jose/page/94/mode/2up

4) Pliny the Younger. (112). *Epistulae X.96*
English Translation: William Whiston.
https://www.pbs.org/wgbh/pages/frontline/shows/religion/maps/primary/pliny.html

5) Tacitus, Cornelius. (116). *Annals* (*Book 15*, chapter 44)
Edited for Perseus, New York by Church, Alfred John and Brodribb, William Jackson. Reprinted 1942. Random House Inc.
http://www.perseus.tufts.edu/hopper/text?doc=Tac.+Ann.+15.44&fromdoc=Perseus%3Atext%3A1999.02.0078

6) GoodShepard Film Production. (2016). Part 2 *Science Explains Shroud Image* NEW 2016 Video [Video]. Youtube.
https://www.youtube.com/watch?v=efEDb2jHyMY

7) Reel Truth History Documentaries. (2019, 11. Sept.). *Turin Shroud: The New Evidence (Shroud of Turin) History Documentary Reel Truth History* [Video]. Youtube.
https://www.youtube.com/watch?v=NVovTvDjjCg

8) *The Israel Museum, Jerusalem.* The Dead Sea Scrolls.
Obtained on February 12, 2021 from:
https://www.imj.org.il/en/wings/shrine-book/dead-sea-scrolls

KODI YESU NDI NDANI? Bukhu ili likufuna kuunikira pa za funso lofunika kwambiriri pofukula mitu ina yokhudza Yesu imene Asilamu ndi Akhristu amayiwona mosiyana:

- Kodi Yesu anafadi pa mtanda?
- Kodi Yesu ndi Mwana wa Mulungu?
- Kodi Yesu iye ndi Mulungu?
- Kodi Yesu ndi Mpulumutsi wa dziko lapansi?
- Kodi Yesu ndiye M'khalapakati wa Mulungu ndi munthu?

Kodi Koran ndi Baibulo zikupereka mayankho otani? Nanga akatswiri owona za mbiri yakale akuti chiyani? Nanga Yesu mwini anati chiyani za izi? Ngakhale kabukuka kali kochepa koma kakusanthula mitu ikuluikulu. Kakuunika mabuku osiyanasiyana ndi kuwafananiza kuti timvetsetse kuti kodi Yesu ndi ndani kwenikweni?



**Titamaliza kuchita zonse ndikuchoka mu moyo uno, funso limene tikayenera kuyankha ndi lakuti: "Kodi unachitapo chiyani za Yesu Khristu?" Kodi unakhulupilira kuti anali mneneri? Munthu wina wakale? Munthu wochita ntchito zabwino? Wamsala ndi wosamvetsetseka? Kapena anali chimene iye amanena kuti anali, Mwana amene Atate kumwamba anamutuma, Mulungu kwathunthu ndi munthu, Yesu Mpulumutsi wa dziko lapansi. Gunna Magga Palsdottir analemba buku lomveka bwino mwa ukachenjede lofotokoza kuti kodi Yesu anali ndani? Musasemphane ndi zabwino chonde werengani bukhuli osati chifukwa chongofuna kusangalatsidwa ndi kalembedwe kake koma pozindikira kuti moyo wanu watsamira pa choonadi chimene chaululidwa mu bukhuli. -Patricia Bootsma**

*Associate Leader, Catch the Fire North, South and Central America*
*Author: Convergence, Raising Burning Hearts, A Lifestyle of Divine Encounters*
*Itinerant Speaker and House of Prayer Leader*

ISBN 978-9935-526-23-6